


CHIZINDIKIRO CHAPAMWAMBA

 [M'bale Neville akuti, "...zopindula zimene Mulungu watibweretsera ife kudzera mu utumiki wanu ndi chikondi. Chimene, pa nthawi ino, ndikufuna kuti ndiziwonetse izo, mwa njira yaying'ono, popereka kwa inu mphatso yaying'ono."—Mkonzi.] Zikomo inu, M'bale Neville. ["Madalitso a Mulungu akhale pa inu, m'bale wokondedwa."] Zikomo inu, kwambiri, M'bale Neville.

² Ndipo zikomo inu, mpingo. Kungoti sindikudziwa zimene ziri mkati mwake. Koma ine ndikuyamikira, ndi mtima wanga wonse, zonse zimene inu mwatanthauza kwa ine, ndi zinthu zimene inu mwandichitira ine. Ndipo mukanapanda inu, sipakanakhalapo ine. Ngati pakanapanda kukhalapo winawake woti azikhulupirira Uthenga umene Mulungu amandipatsa ine kuti ndizilalikirira, sipakanakhala chifukwa choti ine ndizilalikirira Iwo. Pakuyenera kukhala awiri a ife, tikugwira ntchito limodzi. Chotero, ine ndikuyamikira izi kwambiri.

³ Mpingo wathu nthawizonse umakhala ndi, kwambiri kapena pang'ono, pakati pathu pano, chikhalidwe chosangalatsa. Tsopano, pamene ine ndimalowa, basi mphindi pang'ono zapitazo, mchipinda chakumbuyo, winawake anadzandipatsa ine kaphukusi, ndipo anati, kodi ndingafike pa nsanjapo ndi kudzapereka *izi* kwa M'bale Neville. Poyamikira kumverera kwanga kwa iye, ndi chiyanjano cha mpingo uno, ndi chimene iye watanthauza kwa ife chaka chino, ngati m'busa mu zaka zimene zadutsazi, ndi ziyembekezo ndi mapemphero kuti iye apitiriza kukhala m'busa wathu kudutsa zaka zambiri zimene zikubwerazi, chikole kuchokera kwa mpingo ndi ine, M'bale Neville.

⁴ [M'bale Neville akuti, "Zikomo, kwambiri, nonse a inu. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikuyamikira mooni zinthu zachikondi ndi chithandizo chimene chakhalapo kwa ine kuchokera kwa wina aliyense mwa osonkhana. Ndipo moonadi, mmawa uno, ndikumverera pansu mu solo mwanga kuti womalizira aliyense wa ife ndi wothokoza mwakuya kwa M'bale Branham pa chimene iye watanthauza kwa ife, ndi utumiki wake. Ndipo Mulungu amupambanitse iye ndi kumudalitsa iye pamene iye akupitirira ndi Ambuye chaka chino, ndiro pemphero langa lodzipereka. Zikomo, kwambiri. Ndithudi ndikuyamikira izo. Chabwino."—Mkonzi.]

⁵ Ana aang'ono, chabwino, ine ndikuganiza ana tsopano akuyenera kuti azipita ku zawo—zipinda zawo. [M'bale Neville akuti, "Uko nkulondola."—Mkonzi.] Ndipo tsopano kumbukirani, mukakhale atsikana aang'ono ndi anyamata

abwino kwenikweni, uko mchipinda mmawa uno. Pakuti, ukatha msonkhano, ine ndikuganiza zikuwoneka ngati pali chinachake chimene chatsalira kwa inu, zoti tikuchitireni.

⁶ Tsopano, kwa akuluakulu, pamene inu mukuona chathu—chiwerengero chathu cha achinyamata ndi—ndi chokulirapo, ife tikudikirira mwachidwi mpaka nthawi imene ife tidzakhale ndi tchalitchi chatsopano kumene ife tidzalekanitse makalasi amenewo.

⁷ Mlongo wathu Arnold ndithudi ali ndi—ndi wodzadza; osati dzanja lodzadza, koma nkono wodzadza. Ndipo mtsikana wanga wamng'ono amandiuza ine. Iye anati, “Adadi, zimakhala zovuta kwambiri kwa Mlongo Arnold.” Iye anati, “Chifukwa, iye amayankhula kwa ife mu chinenero chimene ife tikhoza kumva, ndipo kenako mwana wamng'ono amakhala akupanga chinachake, ndipo iye amayenera kuimikira kaye ndi kukawakonza iwo, inu mwaona.” Chotero izo zimakhala zovutirapo pa mkazi mmodzi uyu kuti akhale ndi kalasi yonse iyi. Chotero ife tikumuyamikira iye, ndi chake—chimvano chake chabwino pomapanga chimene iye angathe mu nthawi ino yosowa. Ambuye amudalitse iye.

⁸ Tsopano ife tikuyembekezera, tsiku lina, posakhalitsapa, Ambuye akalola, kuti tidzakhala ndi kachisi wamkulu wabwino kumene ife tidzakhale ndi mitundu yonse ya zipinda za Sande sukulu za makalasi. Cha ana aang'ono, chokhala ndi chojambulirapo cha nsalu; ndi kudzachiika icho kuguwa, pamwamba *chonchi*, kwa amakanda kwa galasi lalikulu, kumene namwino wophunzitsidwa azidzakhala kumeneho kuti azikasamalira ana onse. Sikumadzakhala zosokoneza misonkhano, nkomwe, kuyendayenda kapena kuthamanga thamanga pozungulira. Ana aang'ono awa samatopa, ndipo iwo samamvetsa. Iwo amayenera kuwamvetsa iwo. Iwo samatha kutimvetsa ife. Ndipo chotero, ndiye, malo amene chirichonse chingadzakhale basi mwanjira imene ine ndikukhulupirira Ambuye angafunire kuti ife tizichitira. Ife sitidzakhala amanyado, koma tchalitchi chabwino. Ife tikuyembekezera zimenezo.

⁹ Tsopano, kwa M'bale Neville ndi inemwini, ine ndangopezapo lingaliro, awa ndi masuti a zovala. Ine sindikudziwa, M'bale Neville. [M'bale Neville akuti, “Chimenecho, kapena chinachake.”—Mkonzi.] Ine—ine ndikuganiza ndi choncho. Ine sindiri wotsimikiza. Chifukwa, iyo ikuwoneka ngati bokosi la suti, kwa ine. Kodi inu simukumverera chimodzimodzi za izo? Uh-huh. Ndipo izo mwinamwake ndi suti kapena zikhotti. Ndipo ine—ine... Ziwiri zonsezo zikuwoneka chimodzimodzi, chotero izo—izo zikuwonetsera kuti palibe kulemekeza munthu apa. [“Ameni.”] Ndipo, chotero, ine ndiri ndi chikhotti. Ndipo ine ndikudziwa

kuti iwo—iwo...Icho si chikhothi. Chotero icho...Inu muli nacho china, nanunso, chotero iyo ikuyenera kukhala suti. Ndipo ndizo basi...Ife tikungoyamikira izi mochuluka kwambiri! [“Ameni.”]

¹⁰ Ndipo ine ndikutsimikiza, kuti, ngati azibusa, abusa... Mawu akuti *pastor* amatanthauza “m’busa, iye amene amalishya nkhusa.” Ine ndikutsimikiza kuti ife tiri oyamikira kwa inu, wina aliyense wa inu, chifukwa icho chinali—icho chinali chifundo chanu ndi malingaliro, ndi ndalama, zimene zapangitsa kuti mphatso izi zipezeke kwa ife mmawa uno. Ndipo kudzera mu chisomo cha Mulungu, ife tikudzipereka tokha kuti tikhala m’busa wanu, kuti tizichita chirichonse chimene ife tingathe kuti tikutsogolereni inu mu njira yolondola. Mwinamwake, nthawizina, momwe ife timayankhulira ndi zinthu, izo zikhoza kukhala zovuta kuti muzimvetse. Koma ife timangochita izo ngati anamulondola, kuyesetsa kuti tikulondolereni inu ku Malo amenewo, kuti, mu chiukitsiro inu mudzatiyamikire ife mochuluka pamenepo. Pakuti, ife sitinaziganizire ife eni, pochita kudzipangitsa pamene ife tikuyankhula kwa inu, osati malingaliro athu athu, koma timayesetsa kuchita basi mmene Mzimu Woyera ungatitsogolere ife kuti tichitire. Ndipo ndiko... kwakhala kuli kuyesetsa kwathu. Ndipo ife tikuyesetsabe kuti tichite chinthu chomwecho, uko nkulondola, abusa ndi inemwini.

¹¹ Ndife oyamikira kuwona kuwala kwa dzuwa. Doc, m’bale wanga, amangonena kuti iye anatomiza mawu kwa M’bale Frankie Weber, ku Florida, anati, “Si iwe wekha amene angatuluke pa Khirisimasi ndi kumachapa galasi, la galimoto yake, atavala malaya a mikono ake.” Iye anali akuchita chinthu chomwecho, kukufunda kwambiri! Chabwino, inu mukudziwa Florida amatopa ndi kuwala kwa dzuwa, limayang’ana ku Florida nthawi zonse, chotero ilo likuyenera kutulukira ku Indiana ndikuwona mmene chirichonse chikuyendera kuno. Kodi inu simukuganiza chomwecho? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Chotero, ndife okondwa kuti ilo ladzatichezetsa ife, kwa—kwa pafupifupi mphindi pang’ono, mmawa uno.

¹² Koma, pamwamba pa zinthu zonse, ife ndi othokoza chifukwa cha Kuwala kwa Mwana wa Mulungu, kumene kumatipatsa ife kuwalira kwa chisangalalo Chamuyaya.

¹³ Ine ndikudabwa ngati mnyamata wamng’ono, amene akulowa kumene, angafune kuti akakhale ndi makolo ake. Kapena, kuli kalasi ya Sande sukulu kumbuyoko, mnyamata wamng’ono, ngati iwe ukufuna kuti upite kumbuyo uko. M’bale Taylor, kodi inu mungamutsogolere mnyamatayo ku kalasi. Ndi zabwino. Nthawizina iwo amakonda kukhala pawokha, inu mukudziwa. Iwo, iwo amachita zinthu zofanana, zimene

iwo amakonda kumakambirana. Ndipo izo zimangokhala chomwecho basi.

¹⁴ Mtsikana wamng’ono wausinkhu wa zaka thwelofu, monga ine ndakhala ndikunenera kawirikawiri, ngati inu mumuwona wamng’ono wa eyiti-, naini-, usinkhu wa zaka teni akumangoyenda ndi agogo aakazi, nthawi zonse, pali chinachake cholakwika. Mukuona? Pamenepo—pali chinachake cholakwika, chifukwa pali kusiyana kwakukulu mu usinkhu wawo. Inu mukhoza kuganizira kuti, agogowo ali ndi thumba la masuwiti penapake, limene iye akhoza kupisamo dzanja lake. Ndipo mlongo wamng’ono amakhala, maso aakulu awo amangoyang’ana thumba la masuwitiro. Chifukwa, mwa wamba, iwo sangakhale ndi zinthu zoti azikambirana, alibe kalikonse koma basi iye akhoza kumangomuseweretsa iye ndi kumulera iye. Koma umo ndi mmene izo zimakhallira, ndipo ndife okondwa kuti izo ziri mwanjira imeneyo.

¹⁵ Ndiyeno ine ndikunena zimene, ine ndinanenapo nthawi ina, ndikulalikirira za mwanawankhosa ndi nkunda. Inu mwaona, izo zimakhala ndi zinthu zofanana. Izo zikhoza kumakambirana zinthu.

¹⁶ A Masonic, Masonic Lodge, iwo amakhala ndi zinthu zoti akhoza kumakambirana, abale a Masons Lodge; abale a Odd Fellows Lodge. Achi German amakhala nazo zinthu, zoti azikambirana, ku German, za kwawo, pamene achi German akumana wina ndi mzake kumeneko, wina akangobwera kumene kuchokera kwawo. Aku Italy amakhala ndi zinthu zoti azikambirana.

¹⁷ Ndipo Akhristu amakhala ndi zinthu zoti azikambirana. Ndi chifukwa chake ife timasonkhana mmalo ngati ano, mmalo a Mmwambamwamba mwa Khristu Yesu, chifukwa ife ndi mzika za Dziko limodzi. Ife ndi amwendamnjira ndi alendo kuno, ku dziko lino. Chotero ife timakonda kusunkhana pamodzi pa mmawa wa sabata uwu ndi nthawi za msonkhano wa pemphero, kusunkhana tokha pamodzi, chifukwa timakhala ndi zinthu zofanana. Ife timakonda kukambirana zofanana, zinthu zofanana, zimene ife timazikonda: Ambuye, zochita Zake. Winawake, mu mtima mwawo, mukutentha chinachake, Ambuye anawachiritisa iwo, ndipo amangofuna kuti akazinene okha kumeneko, “Mwaona chimene Ambuye achita!” Winawake analandira mdalitso waukulu, ndipo amangofuna kuti apite ku tchalitchi, kukakhala pa chiyanjano cha madalitso awa ndi winawakenso. Mwaona, ndi chifukwa chake ife timakhala ndi zinthu zofanana.

¹⁸ Zikuwoneka kwa ine kuti zowulutsira mawuzi ziri bwino mu tchalitchi, mmawa uno. Izo zikuwoneka kwa ine. Ine sindikudziwa. Mukumakhala kubwerera kwa mawu koteroko muno.

19 Koma ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha zotsatira za chitsitsimutso cha sabata latha. Mukuona? Icho sichinangopereka kukondoweza kuno, koma kozungulira, maiko osiyanasiyana, ife tamva kuchokera kumeneko, kuti Ambuye anali wabwino. Tsopano, ndi kuwotcha milatho yakale, kukonza zinthu, ndi kukalowa mwa Ambuye, kukonzekera kulandira madalitso; ngati nthawi yaing'ono iyo inachita zimenezo, zikanakhala bwanji ngati ife tikanangomapitirira? Mukuona? Chotero, tiyeni icho chisafe. Tizingopitirira kutsanulira zida zochuluka, nthawi zonse, mpaka zisonyezo za utsi ziwonekere kuzungulira padziko, kuti Yesu Khristu ali moyo, ndipo pali moto umene ukuyaka mmitima mwathu.

20 Ine nditatha kupanga kudzipereka kwatsopano, kwa ine mwini, ndi mkazi wanga, ndi zina zotero, ife tawona kuti zinthu zasintha kwathu. Ndipo sitirinso amanjenje monga mmene ife timakhalira, osakhazikika ndi olumpha, "Ife kumalephera kuti tichite *ichi*, ndipo ife kumalephera kuti tichite *icho*." Ife tikungofika pa izo mwakachetechete basi, ndipo tikupanga zochuluka.

21 Chotero, tsopano, pakubwera chaka chatsopano. Ndipo ife sitimakhulupirira mu kutsegula masamba atsopano, ife timangokhulupirira mu kuwotcha akale. Chotero mungodzipatulira nokha kwa Mulungu kudutsa mu chaka chikubwerachi, ife sitikudziwa chimene Ambuye ati atichitire ife.

22 Koma ndife othokoza chifukwa cha aliyense wa inu. Ndine wothokoza kwambiri kwa Mulungu chifukwa cha membala aliyense wa Thupi la Khristu, konsekonse. Ndi mmagawo osiyanasiyana a zikhulupiro, ziribe kanthu momwe iwo angamatsutsane ndi ine, ndine woyamikirabe kuti winawake . . . Ngakhale ngati ine nditaganiza kuti iwo akulakwitsa pang'ono, mu Lemba, komabe akuyesetsa kuima motsimikiza ndi chimene iwo akuchikhulupirira. Ine ndithudi ndi wololera kupirira ndi abale amenewo, ndipo iwo nkumapirira ndi ine mu zolakwitsa zanga ndi zinthu, chifukwa palibepo wa ife amene ali wangwiro.

23 Koma mu Uthenga madzulo ena, pamene ine ndinayankhula za Mulungu akudzilekanitsa Iyemwini pa Pentekoste, pa mphambano ya nthawi, kapena pa msonkhano pamene pankayenera kupangidwa chiganizo, "Ndi mtundu wanji wa Mpingo umene Mpingo Wachikhritsu watsopano uwu ungapangidwa?" Ndicho chimene msonkhano umapangidwira. Ndipo ife tikupeza kuti mu Bukhu la Machitidwe, mutu wa 2, ife tikupeza mtundu wa Mpingo umene unaganiziridwa; mtundu wanji wa Mpingo, Mpingo ungapangidwa wotani, Mpingo uzidzachita chiyani iwo ukadzalandira Khristu. Ine ndikuzikonda zimenezo. Ndipo moonamtima ndikulimbanira Mpingo umenewo umene unakhadzikitsidwa koyamba pa

Tsiku la Pentekoste. Tsopano, Iwo unali wosamvesetseka nthawi imeneyo, Iwo ndi wosamvesetseka pano. Ndipo Iwo udzatero, bola ngati pali tchimo pa dziko lapansi, ndi nkondo yoti imenyedwe, izo zidzakhala zosamvesetseka kwa adani athu, komabe ndi zinthu zofunikira za Mulungu zimene ife tikulimbanira kuti Mulungu atichitire ife.

²⁴ Tsopano, zolengeza, ine ndikuganiza M'bale Neville wapanga kale zimenezo.

²⁵ Ndipo pokhala kunyumba sabata ino, kupemphera ndi kufunafuna nkhope ya Ambuye. Pakuti, mchaka chikubwerachi, mothandizidwa ndi Mulungu, ngati Iye angandithandize ine, ine ndikufuna ndikanikizire nkondoyo mwamphamvu kuposa momwe ine ndinayamba ndapangirapo mmoyo wanga wonse. Ndipo mwinamwake gawo lalikulu la chaka chino likathera ku malo akunja, ndi ku Haiti, ndi mu zisumbu, ndi South America, ndi Afrika, ndi Asia, ndi India, ndi—ndi kumtunda mu Scandinavia. Ndipo zonsezo zikuyenera ziganiziridwe sabata ino, ngati Ambuye alola. Chotero pamene ine ndimverera kutsogozedwa kuti ndichite chirichonse kapena kuti ndipite kulikonse, Ambuye amandituma ine kuti ndikachite izo.

²⁶ Kenako ine ndikatsika ndege, pa nthaka, ndipo pakawoneka ngati apa pakubwera wina, ndipo akuti, “Oh, chipembedzo china *ichi* chachokapo, *ichi* chinapanga izi, kapena *ichi* chinalakwitsa, kapena ife sitikanapanga *izi*, kapena olamulira akuti ife tisakhale ndi msonkhano.”

²⁷ Ndiye ine ndimakonda kuimirira, “Koma ine ndabwera mu Dzina la Ambuye.” Ndipo ine ndimadziwa kuti ameneyo ndi mderekezi, ndiye. Mwaona, izo sichoncho, “Kodi ine ndinalakwitsa?” Ine ndatsogozedwa. Kenako iwe ukhoza kuima ndi mapewa ako pa gudumu, ndi kumamenya nkondoyo.

²⁸ Tsopano, ife tisanatsegule Bukhu, kapena kumufunsa Mulungu kuti atsegule Ilo pamene ife tikuwerenga Ilo, ine ndikufuna kunena chifukwa chimene ine ndikubweretsera Uthenga uwu ku mpingo mmawa uno. Iwo ndi Uthenga wanga wa Khristimasi kwa mpingo. Iwo ndi...ngati Mzimu Woyera ungandithandize ine kuti ndipereke chimene ine ndimakhulupirira za izo. Tsopano, ziribe kanthu kuti izo zinalembedwa bwino chotani mu Malemba, ndipo ndi mochuluka bwanji mmene munthu amazimvera izo, iwo akuyenera kudalirabe pa Mzimu Woyera kuti uzipereke izo kwa anthu. Ndipo izo zikukhala itangotha Khristimasi, pamene inu mwamva nkhani zosiyanasiyana za Khristimasi ndi zo—zolengeza, ndi zina zotero, za mauthenga a Khristimasi. Uwu ukhala wapadera pang'ono, kwa nkhani ya Khristimasi, komabe Mulungu waziyyika izo pa mtima wanga.

²⁹ Ndipo tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu kamphindi chabe, mu Kukhalapo Kwake ndi mithunzi ya chirungamo Chake, kuti tipempho chifundo.

³⁰ O Mulungu, Mpulumutsi wathu Wodala ndi Atate, ife tikuyandikira mpando wachifumu Wanu wachifundo. Mu Dzina la Ambuye Yesu, Mwana Wanu, ife modzichepetsa tikudzipereka tokha mmawa uno, kuti tipereke kwa Inu mapemphero athu ndi kuthokoza kwathu, chifukwa cha zonse zimene Inu mwatichitira ife. Mu sabata yapitayi, makamaka, momwe mitima yachitira njala, ndipo anthu asala kudya, ndipo Mzimu Woyera wawadalitsa iwo, wachita zinthu zazikulu pakati pathu! Odwala achiritsidwa. Ndipo Mulungu wadziwika, kuti Iye ali moyo, ndipo Iye amawakonda anthu Ake.

³¹ Ndipo kuti Mawu akadalibe owona kwambiri, a mneneri, pamene iye anayankhula Mawu a Ambuye Mulungu, pamene iye anati, “Ngati anthu amene aitanidwa ndi Dzina Langa adzazisonkhanitsa okha pamodzi, ndi kupemphera, ndiye Ine ndidzamva kuchokera Kumwamba.” Mawu amenewo ali owona basi monga tsiku limene iwo anayankhulidwa koyamba. Ife tinazipeza izo chomwecho, Ambuye. Tsopano tikhululukireni ife, ife tikupempherera, machimo athu onse, kusakhulupirira kwathu konse, komwe kuli tchimo.

³² Ndipo ife tikupemphera, Ambuye, kuti Inu mubwezeretse kwa ife chikhulupiriro chimenecho chimene nthawiina chinasuntha Mpingo woyamba uja. Sitikupempha mabedi amaluma a wofuwofu, koma tikungopempha chifundo cha Mulungu, ndi Kukhalapo Kwake, ndi madalitso Ake kuti azipita nafe. Kaya zikhala mmunda uno kapena mmunda wakutsidya kwa nyanja, kaya ziri pa chisangalalo, kapena mabedi a wofuwofu, kapena kaya ndi kutsogolo kwa nkondo, ziribe kanthu kumene izo zingakhale, Ambuye, chifuniro Chanu chochetsetsa ndicho chikhumbo chathu chamapeto kuti tikutumikireni Inu. Ingozipangani izo kukhala zomveka kwa ife, O Ambuye, kuti ife tisaphonye njirayo, pakuti ife tikuyenda mu dziko lamdima ndi lakhungu, pakati pa anthu a uchimo akhungu. Chotero, yeretsani njira yathu, Atate, ndipo mutitsogolere ife mmene Inu mungathere, nkhusa za msipu Wanu.

³³ Mulole M’busa wa nkhosazo mokoma ndi modzichepetsa atsogolere anthu Ake, pamene ife tikudikirira pa Inu mmawa uno pa Uthenga wa mmawawu. Mulole Mzimu Woyera uyankhule momveka bwino ku mtima uliwonse ndipo mulole ife tigwire chimene mneneriyo ankachiyankhula, ndipo mmenemo, ndiye, tikakhale ndi madalitso a ulemelero wa Kukhalapo kwa Mulungu, kuti tikatsimikizire Mawu aliwonse. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, Mwana Wanu, Mpulumutsi wathu. Amen.

34 Ine ndiwapempha omvetsera athu mmawa uno, iwo amene ali ndi ma Baibulo, ngati iwo angafune kuti awerenge ndi ine, Malemba, kapena kunditsatira ine pamene ndikuwerenga, ngati inu mungatsegule ku Bukhu la Yesaya. Mneneri Yesaya, ndipo mutu wa 7, ine ndikufuna kuti ndiwerenge gawo la Lemba ili. Mu Yesaya, mutu wa 7, ife tiyambira ndi zokambirana za Mulungu ndi Ahazi, pa ndime ya 10.

Chomwechonso AMBUYE anayankhula kenanso kwa Ahazi, anati,

Upemphe iwe chizindikiro cha AMBUYE Mulungu wako; uchipemphe icho mwakuya, kapena mulitali mmwamba.

Koma Ahazi anati, ine sindipempha, komanso sindiwayesa AMBUYE.

Ndipo iye anati, Mverani inu... O nyumba ya Davide; Ndi chinthu chaching'ono kuti inu mutopetse anthu, koma kodi inu mutopetsanso Mulungu wanga?

Chomwecho Ambuye mwini adzakupatsani inu chizindikiro; Taonani, namwali adzaima, ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo... mudzamutcha dzina lake Immanueli.

Iye azidzadya batala ndi uchi, kuti iye adziwe kukana... choipa, ndi kusa-... kusankha... chabwino.

Pakuti mwanayo asanadziwe kukana... choipa, kapena kusankha... chabwino, dziko limene iwe ukudana nalo lidzasiidwa ndi awiri onse... mafumu.

35 Ngati ine ndinganene phunziro kuchokera umu, kuti nditengepo mutu, ine ndikufuna kuti ndigwiritse ntchito mawu akuti: *Chizindikiro Chapamwamba.*

36 Pamene ife tiri ndi usiku wa mdima kwambiri, ndipo nkumawoneka kuti mu... nthawizina kumakhala mdima kwambiri mu usiku uwu mpaka sitimatha kuwona manja athu patsogolo pathu, ndi nthawi imeneyo pamene mphenzi ya mphanda imawala kwambiri. Iyo imatumizidwa kwa ife kuti idzatiwonetsere kuti pakhoza kukhala kuwala mu mdima.

37 Iyi inali nthawi ya ulamuliro wa Ahazi, mfumu yauthakati. Ndipo ngati inu munazindikira, a—Ambuye sanapereke nkomwe uthengawo kwa Ahazi, koma kwa nyumba ya Davide. “Imvani, O nyumba ya Davide! Ichi chidzakhala chizindikiro.” Chifukwa, iwo anali mu nkondo, abale kumenyana ndi abale, ndipo zinkawoneka kuti linali ora lamdima la maulendo a Israeli ndi umwendamnjira wawo. Koma Mulungu analengeza, kudzera mwa mneneri, chizindikiro Chamuyaya. Tsopano, zizindikiro nthawi zambiri...

38 Anthu amakhala ndi zizindikiro. Ndipo ife tikukhala mu dziko lozadza ndi zizindikiro. Munthu wayesetsa kupeza

chizindikiro china. Munthu wayesetsa, kudzera mu kafukufuku wake wa sayansi, mwa kupambana kwake komwe, kuti apange chizindikiro chimene chingakhale chapamwamba, kapena chikumbutso cha luntha lake, cha mmene iye aliri wamkulu, kapena kuti iyeyo ndi woyambitsa wotani. Iye wachita zimenezo kudutsa mzakazi.

³⁹ Mwa chitsanzo, pamene luntha la mmadzi la mdziko, zaka zina osaposera handiredi zapitazo, ankaganiza kuti iwo anali anzeru kwambiri kuti iwo akanakhoza kupereka kwa dziko chi—chizindikiro cha luso lawo lothyathyalika, kuti iwo akanatha kudzimangira okha sitima imene sipakanakhala funde lalikulu mokwanira limene lingadzamize iyo. Ndipo iwo anaitcha sitima iyi Titanic. Iyo inali chikumbutso chosatha kwa dziko, kuti luso lalikulu lomanga sitima linali litafika pa ungiro, kuti iwo akanakhoza kuwonetsa kwa dziko kuti sitima iyi siingamire.

⁴⁰ Chotero, ndi chitetezero chonse pa luntha la omangawo, ndi zonena zawo ndi zoyankhula, ndi kutsimikizira kwa sayansi kuti sitima iyi siingamizidwe! Ndiye pamene zinthuzo ziperekedwa kwa anthu monga choncho, iwo—iwo amawoneka kuti amakhala otsimikizika kuti chirichonse chiri bwino, bola ngati kafukufuku wa sayansi akunena kuti izo ziri bwino.

⁴¹ Chotero iwo anali akuwoloka nyanja yaikulu mu sitima iyi, pa ulendo wake, ndipo ankamverera otetezeka kwambiri kuti panalibe chinthu chimene chikanawapweteka iwo, iwo anapanga phwando lalikulu loledzera. Ndipo akazi onse ndi amuna amene anali mmenemo, kapena, mwinamwake ambiri a iwo, ine ndikhoza kutero, analedzera; ngakhale, iwo amati, ngakhale woyendetsa ndi kapitawo, ndi onse a iwo. Ndipo oyimba anayamba kuimba a—nyimbo za jazi, zimene zinali nyimbo zapamwamba za tsiku limenelo, monga ife tiliri ndi gwedemula lero. Chifukwa, iwo anali otetezeka, iwo anali mu sitima imene anthu anali atalipatsa dziko chizindikiro cha luntha lawo, kuti, “Sitima iyi ikhoza kupirira funde lililonse kapena nyanja iliyonse.”

⁴² Pamene iwo anali mu phwando loledzera ili, iyo inalunjika ku chifunga. Ndipo mmodzi wa akapitawo ananena, kuti, “Ife tikuyenera tikawone mainjini.” Koma wolamulira wamkuluyo anati, “Isiyeni iyo, ‘Izipita molunjika!’ Ife tikuyenera kuti tikafike ku doko ku chochitika china.” Pamene iyo inali kulowa mu chifunga, ngati kuti iyo inali bwana wa chochitikacho, mwadzidzidzi, iyo inakagunda m’bulu wa chipale, ndipo iyo inapita pansu pa madzi.

⁴³ Ndipo ife timauzidwa ndi wandakatulo amene analemba nyimboyo, “Mulungu, ndi dzanja Lake lamphamvu, amawonetsera kuti dziko ili silingathe kuima.”

44 Chopambana chawo chachikulu chinapita pansi pa nyanja, ndi anthu mahandiredi kuchulukitsa mahandiredi oledzera anali mmenemo. Izo sizingagwire ntchito basi.

45 Anali malemu Adolf Hitler amene anapereka kwa anthu aku German chizindikiro choti iye anali wanzeru, iye ankadziwa zonse za moyo waku nkondo. Ndipo, popanda kumunyozetsa iye, iye ankadziwa zochuluka za izo. Koma iye anawatsimikizira anthu aku German, pomanga chimene ife timachitcha Maginot Line, kapena Siegfried Line, pamene iye anatsanulirapo mabilioni a matani a konkire ndi zitsulo pamodzi. Anawonetsera chidaliro chake mu zimenezo, mpaka iye anasamutsa likulu lake kukakhala ku mzere woyambirira, kumene malo odyera ndi malo a malonda ankachitikira pansi pa nthaka, kumene iwo anali ndi mabilioni a matani a zitsulo ndi simenti. Zinalibe kanthu kuti zikuyenda bwanji, German anali wotetezeka. Icho chinali chizindikiro cha chitetezo. Koma chophulitsira chamakono chinaphulitsira izo ku Muyaya, palimodzi ndi Hitler.

46 Anali Nimrod, tsiku lina, amene ananena kuti iye akanadzamanga nsanja imene ikanadzawabweretsa anthu ake, iye anawonetsera chimene iye akanakwanitsa kuchichita ndi luntha lake. Ndipo iye anali woti amanga nsanja imene ikanadzapita kudutsa mitambo, imene, ngati mkwiyo wa Mulungu ukanati udzabwere konse, iye akanatha kudzamuposa nzeru Iye. Ndi kafukufuku wake wa sayansi, iye amakhoza kuika mathanthwe ndi miyala mwanjira yakuti iye akanawatengera anthuwo ku chitetezero, mwa luntha lake. Koma iyo inagwetsedwera pansi, ndi kusokonezeka kwa malirime, ndipo iwo analephera ngakhale kuti amalizitse nsanjayo.

47 Anali Nebukadinezara amene anamanga makoma a Babeloni, ndipo kenako nkumadzibwekerera za izo. Aakulu kwambiri, mpaka, akavalo sikisi ndi magaleta amatha kuchita mjaha kuzungulira makomawo. Zipata zake zinali zazikulu kwambiri, mpaka amuna amakhetsa thukuta la moyo wawo chifukwa cha izo, kumapuntha mkuwa kuti ukhale zipata zimene zinkalemera mahandiredi a matani; mu mzinda waukulu, iwo ankatenga gulu la anthu kuti azitsegule izo. Panalibe amene ankamukhudza Nebukadinezara. Koma usiku wina, mu phwando loledzera, akuganiza kuti iwo anali otetezeka kuseri kwa makoma awo a sayansi, ndi zida za tsiku lawo, panadzabwera cholembedwa ndi Dzanja pakhoma. Ndipo izo zinatha.

48 Oh, momwe munthu wayeserera kuti amutengere munthu ku chitetezero, kuzikankhira yekha ku chitetezero, mwa zizindikiro zake zomwe za kuchitabwino. Izo zikuwoneka ngati, chifukwa choti anthu amafuna chizindikiro, pakuyenera kukhala chifukwa cha izo; chinachake mkati mwa munthu

chimene chingaitanire chifukwa chake kapena chizindikiro, kuchokera kwina kwake, kuti iye akhale wotetezeka.

⁴⁹ Kenako Mulungu anadzayankhula, anati, “Ine ndiwapatsa iwo chizindikiro chosatha. Ine ndiwupatsa Mpingo chizindikiro chosatha.” Icho sichinali kuti chidzakhala khoma kapena nsanja. Iye anati, “Namwali adzaima, ndipo adzabala Mwana, ndipo adzamutcha Dzina Lake ‘Immanueli.’ Chimenecho chidzakhala chizindikiro cha Mulungu Chamuyaya.” Zophweka bwanji! Zochepa bwanji!

⁵⁰ Kodi inu mukumvetsa kuti ndi zinthu zazing’ono zimene inu mumazidumpha ndi kuzisiya, zimene zimatanthauza mochuluka kwambiri kwa Mulungu? Kodi mpingo ungaganizire zimenezo mmawa uno? Mu kupambana kwathu ngati bungwe, ndi nyumba zake zazikulu ndi mbambande, ife tikumalambalala zinthu zazing’ono zimene zimatanthauza mochuluka kwambiri kwa Mulungu ndi mochuluka kwambiri kwa kopita kwathu Kwamuyaya. Ife timazilambalala zinthu zimenezo.

⁵¹ Mulungu akunena, kuti, “Ine ndikupatsani inu chizindikiro Chamuyaya. Namwali adzaima, ndipo adzabala mwana.”

⁵² Bwanji, chifukwa chiyani mwana, nchifukwa chiyani akuyenera kukhala mwa—mwana? Mlengi Iyemwini amayenera kubwera ndi kudzakhala mu chirengedwe Chake, kuti zidzakhale chizindikiro kwa munthu? Nchifukwa chiyani akuyenera kukhala mwana? Bwanji Iye sananene kuti, “Ine ndimanga makwerero aakulu, ndipo nonse a inu . . . monga loto la Yakobo. Kapena, Ine ndidzatsitsa kuchokera Kumwamba, kuchokera mmakonde a Kumwamba, chingwe, ndipo ndidzakupatsani inu mphamvu, kuti, inu mukadzimangirire nokha kwa icho, Ine ndidzakukokereni inu mmwamba?”

⁵³ Koma, Iye anabwera mophweka kwambiri. Ndipo anati, “Mwana adzabadwa. Chimenecho chidzakhala chizindikiro. Icho sichidzakhala chizindikiro chokha, koma icho chidzakhala chizindikiro chapamwamba.” Mwana! Bwanji, luntha la sayansi lidzaseka pa nkhope ya ganizo loterolo. Koma, kwa Mulungu, icho chinali chizindikiro chapamwamba. “Namwali adzaima, ndipo mwana uyu adzatchedwa *Immanueli*, limene mwakutanthauzira lidzakhala, ‘Mulungu nafe.’” Chimenecho ndicho chizindikiro chapamwamba.

⁵⁴ Mulungu Wakumwamba, kumakhala ndi anthu, ndi chizindikiro chapamwamba. Icho sichidzangokhala chizindikiro cha tsiku limenelo, koma cha tsiku lino ndi cha masiku onse, kuti Mulungu amakhala ndi anthu Ake. Immanueli, Mulungu nafe, ichi ndi chizindikiro chapamwamba. Ichi ndi chizindikiro Chamuyaya, chizindikiro chosatha, Mulungu anachipereka.

⁵⁵ Ndipo nchifukwa chiyani Iye anadzakhala fumbi, fumbi kumene la chirengedwe Chake Chomwe? Mlengi anadzakhala chimenecho, fumbi la chirengedwe Chake.

⁵⁶ Munthu amayesetsa kuchita chinthu chachikulu chopambana. Koma, pamene Mulungu anadzapereka chizindikiro, icho chinali chinthu chaching'ono. Munthu amayesetsa kuchita ndi zochitika zazikulu. Mulungu amachita ndi chochitika chaching'ono. Munthu amayesetsa kumati, “Chifukwa aliyense akupita njira *iyi*, tiyeni tichite monga iwo akuchitira izo ku Hollywood.” Mulungu amafuna apang'ono. Iye amafuna ku—kuchotsa zinthu zonse zazikulu, kuti akalandire chaching'onocho.

⁵⁷ “Mwana adzabadwa, Immanueli wamng'ono adzabadwa.” Mulungu wachirengedwe anadzakhala gawo la chirengedwe Chake Chomwe. Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, Amene anapanga fumbi ndi mitengo, ndi zinthu zonse zimene ziripo, kudzakhala gawo la izo. Chimenecho chidzakhala chizindikiro, Iye adzadzera njira ya munthu.

⁵⁸ Tsopano, Iye akanakhoza kudzera njira ina. Iye akanakhoza kudzera mwa njira ya zina, ya—ya njira zina zomwe Iye ali nazo zodzera.

⁵⁹ Koma Iye anasankha kudzera njira iyi, kuti adzapereke chizindikiro, chizindikiro chapamwamba. “Namwali adzaima, ndipo adzabala Mwana, ndipo iwo adzamutcha Iye ‘Immanueli.’” Tsopano, icho chinali cha chiyani? Chifukwa chiyani?

⁶⁰ Nchifukwa chiyani Iye sanasankhe kudzakhala Mngelo? Iye akanakhoza kuchita zimenezo. Iye akanakhoza kubwera mu—munthu wokhwima wamkulu. Iye akanakhoza kubwera ndi sawasha yathunthu kuchokera Kumwamba, ndi Angelo ndi Zolengedwa zonse za Kumwamba; kutsika pansi kuchokera mmakonde Akumwamba, makwerero agolide, ndipo Iye akanakhoza kudzatsika pansi ndi gulu la Angelo. Iye akanakhoza kuchita zimenezo.

⁶¹ Koma Iye anati, “Ine ndikupatsani inu chizindikiro, chizindikiro chapamwamba, chizindikiro chosatha. Namwali adzaima, ndipo adzabala mwana.”

⁶² Ndipo pamene Iye ankayenera kuti asankhe malo oti mwana uyu adzabadwire. Iye akanakhoza kutsika pansi pa makwerero, ndi sawasha yathunthu Yakumwamba. Iye akanakhoza kubwera kuchokera Kumwamba ngati Mngelo, kapena kubwera pansi ngati bambo wokhwima wathunthu. Koma Iye, aponso, akanakhoza kudzafikira ku nyumba ya mfumu.

⁶³ Koma Iye anati, “Ine ndipereka chizindikiro.” Ndipo chizindikirocho chinanenedwa kwa abusa, “Inu mukampeza Iye mkhola, atakulungidwa mu zovala zapagoli.” Chimenecho ndicho chizindikiro chapamwamba, wobadwira pa mulu wa ndowe, ndi kununkha kwa mkhola, wopanda ngakhale zovala zoti amuveke Iye, Immanueli. Mdierekezi amafuna

kuzipanga zinthu kukhala zazikulu ndi zowala. Mulungu amadzichepetsa zinthu. Chizindikiro chapamwamba, “Inu mukampeza Mwanayo atakulungidwa mu zovala zapagoli, atagona modyetsera. Ichi chidzakhala chizindikiro, chizindikiro chapamwamba.” Pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye anali wosauka kwambiri. Ife timakamba chotani nthawi yovuta? Kodi wamng’ono Uyu ndi ndani? Ndi Yehova!

⁶⁴ Yehova Mulungu anadzakhala munthu, anatenga mawonekedwe athu, anadziwolotsa Yekha kuchokera kwa Mulungu, ndipo anadzakhala munthu. Ndi chimenecho chizindikirocho. Anadzakhala...Iye anali Mulungu, ndipo anadzakhala munthu; osati munthu wolemara, koma munthu wosauka. Ichi ndi chizindikiro chapamwamba. “Inu mwafunsa chizindikiro,” anatero Mulungu, “Ine ndikupatsani inu chimodzi, chizindikiro chosatha.”

⁶⁵ Iye akanakhoza kubwera mwanjira ina, monga ine ndanenera, koma, mwana, nchifukwa chiyani Iye anadzakhala mwana? Pamene kamwa loyamba laling’ono lija, lopanda mano linatseguka mkholamo, pa kabedi koyamba ako... mmawa woyamba wa Khristimasi, mu kabedi Kake kakang’ono ka mkhola, ndipo kulira kwake koyamba kumene kunapita kuchokera ku liwu Lake, ameneyo anali Mulungu akulira. Yehova akulira, munthu; anabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo anali munthu, gawo lililonse, munthu. Anabwera ku dziko lapansi wopanda kalikonse, komabe anali munthu. Kodi Iye anali kuyesetsa kuti achite chiyani? Iye amalinga chiyani?

⁶⁶ Iye amalira ngati mwana, mu khola. Iye amasewera ngati mnyamata, pa msewu. Iye anavutika ngati munthu, komabe Iye anali Immanueli. Ichi ndi chizindikiro chapamwamba. Mulungu akukhala mu chirengedwe chimene Iye anachirenga. Chizindikiro chapamwamba, “Icho chidzakhala chizindikiro kwa inu.”

⁶⁷ Iye anali wosauka kwambiri, pamene Iye anadzabwera pa dziko lapansi, Iye anabwera kudzera mu chiberekero chobwerekera, chiberekero chobwerekera cha mkazi. Ndipo anachita kubwerekera manda, kuti adzaikidwemo. Mulungu! “Namwali adzaima, popanda chochitika cha kugonana.” Yehova anabwerekera chiberekero cha Maria, mkazi, kuti adzachite ntchito yoti Iye adzapereke chizindikiro chosatha. Ndipo anali wosauka kwambiri, pa dziko lapansi, zitatha zaka sate firii ndi theka, za utumiki, Iye anachita kudzabwerekera manda kuti ayikidwemo. Kodi inu mungaganizire? Mukuyankhula za kutenga mimba kwachiyero, inu mukutanthauza chiyani, mulimonse?

⁶⁸ Kodi inu simukuchiwona chizindikiro chenichenicho? Ndi Yehova kudzakhala mmodzi wa ife. Yehova Mulungu pa dziko lapansi, ngati wothawathawa, mwendamnjira mu dziko limene

Iye analilenga; wokanidwa, ndi wokankhidwa, ndi wosekedwa, ndi wonyozedwa; Mwala wopunthwitsa kwa wosakhulupirira, Thanthwe lolakwitsa; mdierekezi, kwa dziko lachipembedzo. Koma chizindikiro Chamuyaya kwa wokhulupirira, “Mulungu nafe,” chizindikiro chapamwamba. Kodi inu mukuchiwona icho? Mulungu anawonetseredwa, Mulungu anadzipereka Iyemwini kwa dziko, ngati wothawathawa. Akanatha kubwera mwanjira ina, koma anasankha kuti abwere mwanjira iyi.

Mvetserani kwa Ichi. Musachiphonye Ichi.

⁶⁹ Ine ndikuganiza kuti Mulungu anali nazo mmalingaliro Ake, izo zingakhale zokopa kwa munthu. Izo ziri, kwa wokhulupirira. Izo zimakhala zokopa pamene Mulungu wathu akhala mmodzi wa ife. Koma, kwa wokhuthala, wopanda umulungu, chopunthwitsa. “Ine ndidzakupatsani inu chizindikiro, namwali adzaima. Immanueli adzakhala ndi inu.” Mulungu ankaganiza kuti izo zikanadzakhala zokopa kwa mtundu wa anthu, kuti Mulungu wathu adzakhala mmodzi wa ife, kuti Iye adziwoloketsa Yekha ndi kudzakhala fumbi lathu, kuti Iye adzakhala thunthu lathu, thunthu la munthu; Mlengi Amene anapanga zinthu zonse.

Ndipo, kenanso, izo zinakwaniritsa ulosi. Aneneri anali ataziwona izo.

⁷⁰ Ndipo chinthu china, “Mawu anasandulika fumbi, mnofu, ndipo anadzakhala pakati pathu.” Yehova, Mawu anadzakhala munthu, anadzakhala fumbi ndipo anadzakhala mkachisi limodzi nafe. Chizindikiro *chosatha*, “sichidzatha konse.” Oh, pamene ife tiganiza za zimenezo, chizindikiro Chamuyaya, zizindikiro zapamwamba za chizindikiro chonse. Mulungu kudzakhala mmodzi wa ife.

⁷¹ Ndiye, kenanso, Iye akuyenera kukhala Mbewu ya Abrahamu. Abrahamu, ndithudi, anali mbewu ya Eva. Eva. . . “Anali Mbewu ya mkazi imene imati idzavulaze mutu wa serpenti.” Koma, Abrahamu, ngati inu mungazigwire izi, iye anali ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, zimene zinalumikiza Mzimu wa Mulungu ndi thupi la munthu. Pamenepo ndi pamene chikhulupiriro chinadzabwera. Pamenepo ndi chifukwa Iye akanadzakhala Mbewu ya Abrahamu, osati thupi lonse, koma kulumikizana kwa Mzimu ndi thupi pamodzi. Mulungu, kudzipanga Iyemwini. . . kuphwasula, kuzulapo choipa chonse, kulibweretsa thupilo kuti lizimvera, fumbi limene Iye analilenga, ndi kumakhala ndi inu ngati a—bwenzi.

⁷² Chinthu china, Iye sanawononge nkomwe kapena kutsutsa lililonse la malamulo Ake. Iye sangachite zimenezo. Chotero, “Namwali. Ine ndikupatsani inu chizindikiro.” Osati Titanic, osati U.N., koma, “Ine ndikupatsani inu chizindikiro cha chitetezero. Namwali adzaima, ndipo iye adzabala Mwana

wamwamuna, ndipo adzamutcha Iye ‘Immanueli.’” Chimenecho ndicho chizindikirocho. Inde.

⁷³ Inu mwawona, mu malamulo a Mulungu a chiwombolo, monga izo zinakhallira ndi Boazi ndi Naomi, an kayenera kukhala wachibale wapafupi. Ndipo njira yokhayo imene munthu akanadzawomboledwera, Mulungu an kayenera kuti adzakhale wachibale, wapafupi. Ine ndikufuna kuti inu muziwone zimenezo. Iye sanadzakhale achibale, pamodzi, kwa olemera, kwa amphamvu. Koma Iye anabawira mkhola, anakulungidwa mu zovala zapagoli; osati kwa wamkulu, koma kwa mwana. Iye anali Mulungu pamwamba pa chirengedwe. Iye anasankha kuti adzachite zimenezo, osati kubwera ngati munthu wathunthu wokhwima. Iye anabwera kuti Iye adzathe kuzuzika ndi kumverera kwa makanda. Iye anabwera kuti Iye adzathe kudutsa mayesero a wa mzaka za mmatini. Adzathe kupita, kuti Iye adzavutike ndi zovuta ndi misampha ya mdierekezi, ngati munthu, ndi kudzapanga njira kwa anthu a mibadwo yonse, misinkhu yonse ndi magulu onse: osauka, olemera, onse. Iye anadzakhala wosauka, kuti, kudzera mu umphawi Wake, ife tidzathe kukhala olemera ndi olandira limodzi ndi Iye mu Ufumu. Chizindikiro chidzaperekedwa, akuzidutsitsa Yekha, akudzipanga Yekha kukhala chinachake chosiyana ndi chimene Iye anali; tsopano chizindikiro chapamwamba, akulira ngati mwana, akusewera ngati mnyamata, akuvutika ngati munthu, koma anali Mulungu akukhala magawo onse a moyo monga ife timachitira.

⁷⁴ Inu mukudziwa, Mulungu wapereka zizindikiro zambiri zoti Iye anali Mulungu. Iye anapereka chizindikiro kwa dziko lachigumula, kuti Iye anali Mulungu, Mulungu wa chiweruzo. Iye anawamiza anthu mmasiku a Nowa, ndipo anawayandamitsa olungama mu chombo; chizindikiro choti Iye anali wolungama, ndipo chiweruzo chinali chotsimikizika. Chimenecho ndi chizindikiro, kuti wochimwa wosalapa aliyense adzawonongedwa mu chiweruzo, kuti olungama adzapulumutsidwa mwa chifundo cha Mulungu.

⁷⁵ Iye anapereka chizindikiro china pa chitsamba chonyeka. Kodi icho chinali chiyani pamene Iye anamugwira mneneri wake wothawa, “Ine ndamva kulira kwa anthu Anga, ndipo Ine ndakumbukira pangano Langa”? Iye anapereka chizindikiro china pamenepo, kuti Iye anali Mulungu wosunga pangano, kuti Iye anakumbukira chirichonse chimene Iye ananena, lonjezo lirilonse limene Iye analipanga. Anapereka chizindikiro pa chitsamba chonyeka, “Ndipo Ine ndabwera kudzawawombola iwo.”

⁷⁶ Muwoneni Mulungu mu njira Zake za ntchito. Pamene Iye analenga Miyamba ndi dziko lapansi, Iye anawaitanitsa Angelo pamodzi, ndipo Iye anati, “Tiyeni ife.” Malo aliwonse mu Lemb

pamene Iye akupanga chirichonse, kawirikawiri, “Osati Ine, koma Atate Anga.”

⁷⁷ Koma pamene izo zinadzafika ku dongosolo la chiwombolo, Iye anadzabwera yekha. Panalibe amene anali ndi Iye. Iye anali Mmodzi yekhayo amene akanabwera. Mngelo sakanadzachita zimenezo. Munthu wina, wotchedwa mwana Wake, sakanadzachita zimenezo. Wina wotchedwa chinachakenso, namwali woyera, kapena mayi woyera, kapena—kapena woyera winawake, sakanadzachita izo. Mulungu ankayenera kuti abwere! “Ndipo Ine ndidzakupatsani inu chizindikiro. Namwali adzaima; ndipo mwana adzabadwa, ndipo Iye adzakhala Immanueli, Mulungu nafe,” chizindikiro chapamwamba. Mulungu mwa anthu Ake. Mulungu ndi anthu Ake. Mulungu anadzakhala anthu Ake. Mulungu ndi munthu anadzakhala mmodzi. Chizindikiro! Chopunthwitsa kwa dziko, koma chiyembekezo chodala kwa wokhulupirira. Chizindikiro chimene chidzayankhulidwire zoipa.

⁷⁸ Iye anali ndi nthawi ina imene Iye anatsimikizira. Iye anatsimikizira mu chigumula kuti Iye anali Mulungu wa chiweruzo, ndi Mulungu wa chifundo kwa iwo amene amasunga Malamulo Ake.

⁷⁹ Iye anawonetsera pa chitsamba chonyeka, mwa chizindikiro, kuti Iye akanadzazunga lonjezo lililonse limene Iye analipanga.

⁸⁰ Ndipo pa Nyanja Yofiira, Iye anawonetsera kuti Iye adzapanga njira kwa iwo amene akuyesetsa kuchita zabwino ndi kutsatira Lamulo Lake. Ziribe kanthu chimene chikudula izo, Mulungu anatsimikizira pa Nyanja Yofiira, ndipo anadzapereka chizindikiro, kuti Iye akhoza kutsegula nyanja. Mu yesero lililonse, Iye adzapanga njira yothawirapo. Mukuti, “Amayi sakukhulupirira Izo. Adadi sakukhulupirira Izo. Mpingo sukukhulupirira Izo.” Ine sindikusamala amene sakukhulupirira Izo. Ngati inu mukukhulupirira Izo, Mulungu adzakupangirani njira yothawirapo. Iye anapereka chizindikiro kuti Iye akanadzatero. Iwo anali ali pa njira yawo, molunjika wa ku dziko lonjezedwa, kumene Mulungu anawalonjeza iwo. Ndipo Nyanja Yofiira inawatsekereza iwo, ndipo iwo anakhala mu vuto. Iwo sanadziwe choti achite. Mulungu anawonetsera kuti Iye adzapanga njira yothawirapo mu yesero lililonse, yesero lililonse. Inu mukulephera kusiya kusuta? Dزامutengeni Mulungu nthawi ina. Inu mukulephera kusiya kunama, mukulephera kusiya kuba, mukulephera kusiya kupsya mtima? Mudzamutenge Mulungu ndi inu nthawi ina. Ngati inu simukumverera ngati kuti mupite ku tchalitchi, ndipo mukulephera kupita kulikonse; mudzamutenge Mulungu ndi inu kamodzi, mudzatenge lonjezo Lake. Iye anatsimikizira, pa Nyanja Yofiira, kuti Iye adzapanga njira yothawirapo. Mulungu wapereka zizindikiro zambiri.

⁸¹ Usiku umenewo pamene Iye ananena kwa azibusa, “Mupite uko ku Betelehemu, pakuti tsiku ili kwabadwa Khristu Mpulumutsi. Khristu, Mulungu wodzodzedwayo, tsiku ili wabadwa mwa mkazi.” Mulungu!

⁸² Osati kumupanga iye kukhala mulungu, tsopano. Iye anangobwerekera chiberekero cha mkaziyo, chimodzimodzi mmene Iye amabwerekera thupi *ili* kuti alalikiremo Uthenga. Chimodzimodzi monga Iye amabwerekera thupi lanu, kuti akachite ntchito imene Iye akufuna kuyipanga kudzera mwa inu, chifukwa Iye akadalibe Immanueli, chizindikiro, Mulungu ndi anthu Ake. Mulungu kumakhala pakati pa anthu Ake, chizindikiro chapamwamba, chosatha. Icho sichingalephere konse. Icho nthawizonse chidzakhala chizindikiro.

⁸³ Inu mukukamba za zizindikiro izi, nanga bwanji ichi? Inu musanapeze konse chizindikiro china chirichonse, chizindikiro choyankhula mmalirime, chizindikiro cholosera, chizindikiro cha chاوزimu chirichonse, inu mudzayenera kubwerera ku chizindikiro chapachiyambi, chizindikiro Chamuyaya ndi chosatha. Mupite molunjika, kuyamba ndi kuyamba, ndipo pa maziko amenewo, amene ali Thanthwe la mmibadwo, ndipo palibe kanthu kadzagwire icho. Zipata za Gehena zidzatsutsana ndi icho, koma sizingagonjetse. Kapezeni chizindikiro chimenecho, “Namwali adzaima, ndipo adzabala Mwana.”

⁸⁴ Ndipo Iye anawauza azibusa awa, “Apa ndi mmene inu muti mukamupezere Iye. Iye akakhala modyetsera, mkhola, atakulungidwa mu chovala chapagoli. Ndipo pamene inu mukayang’ane pa Iye, mukakhulupirire, pakuti Iye ndi Mulungu pakati pathu.”

⁸⁵ Chizindikiro chimenecho sichinali kwa azibusa okha. Koma icho chinaperekedwa kwa dziko lonse, kuti likayang’ane pa Iye ndi kuwona kuti Iye ndi ndani. Ndi Mulungu nafe, Immanueli.

⁸⁶ Pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anatsimikizira kuti Iye anali Mulungu. Anatsimikizira kuti Mulungu anali mwa Iye, chifukwa zizindikiro za Mulungu zinkamutsatira Iye. Iye anati, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine. Koma ngati Ine ndikuchita ntchito za Atate Anga, ngati inu simukundikhulupirira Ine, mukhulupirire ntchitozo, chizindikiro.” Immanueli! “Ine ndi Atate Anga ndi mmodzi. Atate Anga andituma Ine. Ndipo monga Iye akundituma Ine, chomwechonso Ine ndikukutumani Inu. Atate, wandituma Ine, akukhala ndi Ine. Iye ali mwa Ine ndipo akuchita ntchito za Iyemwini. Ndi Mulungu mu thupi.”

⁸⁷ Kodi Loti sanalawe zimenezo chiwonongeko chisanachitike? Pamene, iye anamuwona Mulungu akuwonetseredwa mu thupi, akudya nyama, akumwa mkaka wa ng’ombe, akudya mkate wochokera mu uvuni, ndipo anaima nsana Wake

atautembenezira ku hema, ndipo ali ndi puronauni ya umwini “Ine.” “Ine, powona kuti Abrahamu ndi wolowa wa dziko, ine. . .” Mwa kuyankhula kwina, “Ine ndimudziwitsa iye.”

⁸⁸ Iyeyo anali ndani? Ndiye Iye anati, “Abrahamu, ali kuti mkazi wako, Sarah?” Izo zinamudzidzimutsa iye. Mulungu, mu chithunzithunzi cha Khristu, anasandulika thupi.

Anati, “Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanu.”

Sarah anaseka. Ndipo Iye anati, “Nchifukwa chiyani Sarah waseka?”

⁸⁹ Pamene Immanueli anabwera kudzera mu chiberekero cha mkazi, mmalo mowonekera ngati fiyofane, Iye anati, “Monga izo zinali mmasiku a Loti, chomwechonso izo zidzakhala pakudza kwa Mwana wa munthu.”

⁹⁰ Pamene Iye anali pa dziko lapansi, atumwi amenewo ankapita ndi Uthenga, mwakuti ngakhale Angelo anasuzumira kudutsa chotchinga cha Kumwamba, makonde a Dziko la Ulemelero, kuti ayang’ane Izo. Inu amene mukulemba Lemba, monga ine ndikukuwonani inu mukulemba, Timoteo Woyamba 3:16. “Popanda kutsutsana chachikulu ndi chinsinsi cha umulungu: pakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi, anakhulupiridwa mu dziko, anawonedwa ndi Angelo.” Angelo anadzuka kuti amuwone Mulungu. Iwo nthawiina anakupizapo ndodo zawo pamaso pa Iye, akufuula, “woyera, woyera, woyera,” pamene Iye anali atakhala Pamenepo, ngati Lawi la Moto, mu ulemelero wa Kumwamba. Ndipo pamene Iye anadzakhala munthu, Angelo anadzabwera ndipo anadzasuzumira kuti amuwone Iye, Yehova, atasandulika thupi. Ndithudi, “Popanda kutsutsana chachikulu ndi chinsinsi cha umulungu.”

⁹¹ “Ine ndidzakupatsani inu chizindikiro chosatha,” pakuti Mulungu anasandulika thupi pakati pathu. Iye anadzakhala mu thupi. Icho chidzakhala chizindikiro chosatha. Osati kokha kwa azibusa kuti awone ndi kukhulupirira, koma kwa inu Branham Tabernacle, ndi kwa dziko lankhanza ili, kuti likhulupirire kuti ameneyo ndi Mulungu. Mulungu anapereka chizindikiro chimenecho. Yesu anati, “Monga Atate amoyo anditumiza Ine, ndipo wabwera ndi Ine, ndipo anali mwa Ine; chomwechonso Ine ndikukutumani inu, Atate amoyo kuti apite ndi iwe ndi kukakhala mwa iwe, chizindikiro chosatha. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Onani, Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumapeto a dziko lapansi. Ine ndidzakhala ndi inu. Mapeto a dziko lapansi, Ine ndidzakhala kumeneko ndi inu.”

⁹² Winawake, monga ine ndanenapo mmbuyomo, akufuna kumupanga Iye kukhala Mulungu wamng’ono, wamfupi. Iye anali munthu; Mulungu anali kumugwiritsa ntchito munthu. Mulungu anali kugwiritsa ntchito thupi limene Iye analilenga, Iyemwini, ndi cholinga chakuti adzalenge kudzera mwa Iye,

“Ndi kuti adzabweretse kudzera mwa Iye ana ambiri,” Lemba limatero, “kudzera mwa Mwana womvera uja. Kudzera mwa mwana mmodzi, onse anagwa. Kudzera mwa Mwana womvera, onse adzakhala moyo, amene akhulupirira.”

“Mulungu nafe,” chizindikiro, ananena kuti icho chidzakhala chizindikiro. Iye anakonda kwambiri kumadzinena Yekha ngati “Mwana wa munthu,” munthu Iyemwini, munthu basi. “Ine si kanthu; Mwana sangachite kalikonse mwa Iyemwini.” Koma ndi Atate amene anali mwa Iye, Immanueli, Mulungu.

⁹³ Mwa—mwana, Mulungu, Yehova Mulungu. Khanda laling’ono lija linalira, ameneyo anali Yehova. Kodi inu mukuziwona zimenezo? Mulungu kumakhala mwa khanda.

⁹⁴ Mulungu kumakhala moyo mwa wa zaka zammadini. Kodi Iye anali wa zaka zammadini wotani? Iye anawonetsera chitsanzo. Pamene Iye anatayana ndi abambo Ake ndi mayi Ake, iwo anamuyang’anayang’ana kuti amupeze Iye, ndipo iwo anakamupeza Iye mu kachisi. Kodi Iye ananena chiyani, ngati wa zaka zammadini? “Kodi inu simukudziwa? Simukudziwa kuti Ine ndikuyenera kukhala pa ntchito ya Atate Anga?” Chitsanzo kwa ana a zaka zammadini.

⁹⁵ Ngati munthu, ndi zapamwamba zonse za mdziko zitaperekedwa kwa Iye, chirichonse chiri mmanja Mwake, kuti adzakhale wamkulu pa amuna onse, wolemera kwambiri wa anthu onse; Amene amakhoza kuwauza anthu kutenga nsomba inali ndi khobidi mkamwa mwake, kukhoza kutenga madzi abwino kuchokera mu zitsime ndi kuwasandutsa iwo kukhala vinyo, amene ankatha kusintha chirichonse chimene Iye akufuna kuchisintha; amene amakhoza kutenga mabisiketi asanu ndi kudyetsa zikwi zisanu. Ndi mphamvu mmanja Ake kuti adzakhale munthu wopambana, komabe anasankha kukhala wosauka. Analibe ngakhale manda pamene Iye ankafa. Iye anachita kubwera amodzi. “Immanueli, ichi chidzakhala chizindikiro.” Kodi Mulungu amabwera motani? Mwa osauka. Kodi Mulungu amachita motani? Icho chidzakhala chizindikiro chosatha, ndi osauka, osaphunzira.

⁹⁶ “Chizindikiro,” anatero mneneri wamkazi wamkulu, Ann, pamene Simioni anakweza manja ake mkachisi, ndipo atamuyangata wamng’ono Uyo ali mu chovala chapagoli. Ann akuti, “Icho ndi chizindikiro chimene chidzanenedwere zoipa, pa kugwa kwa Israeli, koma kusonkhana pamodzi kenanso, aponso, Kuwala kwa Amitundu.”

⁹⁷ Chiyani? “Mulungu nafe,” osati mwa olemera ndi odzitamandira, koma mwa osauka. Anabadwira mu khola, “Mulungu nafe.” Kodi Iye anachita zinthu za mtundu wanji? Penyani zinthu Zake zimene Iye ananena. Mpenyeni Iye, chimene Iye ananena.

⁹⁸ Pakuti, Mulungu Iyemwini anati, “Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa, mvereni inu Iye. Uyu ndi Mwana Wanga Yemwe Ine ndikukondwera kukhalamo. Mvereni inu Iye.” Iye anati, “Ine ndidzakhala ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka kumapeto.”

⁹⁹ Iye anatumiza akuphonzira Ake. Iwo analitentha dziko, mmasiku awo, monga Mulungu kukhala mmodzi ndi munthu. Iwo amawabatiza anthu mu Dzina la Mulungu ameneyo, Yesu Khristu. Iwo ankakhala pafupi kwambiri ndi Iye mpaka Iye amadziwonetsera Yekha kudzera mwa iwo, kudzera mu zizindikiro ndi zodabwitsa ndi mphatso za Mzimu Woyera. “Mulungu nafe.” Iwo anali kulalikirira kuti panali Mulungu mmodzi woona ndi wamoyo.

¹⁰⁰ Munthu wamanga mitundu yonse ya nsanja pa milungu itatu kapena inai, kapena milungu iwiri, koma alipo Mulungu mmodzi. Uthenga umenewo unali woti udzatsitsimutsidwe mu tsiku lotsiriza.

¹⁰¹ Inu mukuyenera muvule kuganiza kwanu tsopano, mutsegule mitima yanu. Mumufunse Mulungu kuti awulule ichi kwa inu, chimene ine ndikukonzekera kuti ndichinene.

Pamene Iye anadzabwera, Iye anakwaniritsa zimene mneneri ananena.

¹⁰² Ndipo pamene Iye akubwera mmasiku otsiriza, mu mvula yamasika ya Mulungu, pamene ziwiri zonse mvula ya nyundo ndi yamasika zidzavumbitsidwe, Iye akubwera ndendende basi mmene izo zinaloseredwera za Iye. “Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kwamadzulo.” Kunkayenera kudzachitike chiyani? Immanueli, Mwana yemwe uja, Kuwala komwe kuja, Mulungu yemwe uja amene anabwera kudzakhala mu thupi, ndi anthu Ake pa Tsiku la Pentekoste, adzabwera mwa chikhalidwe chomwecho mmasiku otsiriza, pakuti kudzakhala Kuwala kwamadzulo. Ndi chiyani chimenecho? Padzakhala chizindikiro, chizindikiro chosatha: Mulungu nafe, Mulungu mwa ife, Mulungu kudzera mwa ife. Munthu ndi Mulungu kudzakhala mmodzi. Yesu anafa, mwakuti Iye anapereka moyo wofunika umenewo, pa chigamulo Chake. (Mu Uthenga wa Lamlungu lapitali.) Chifukwa, Iye anaupereka iwo ngati chigamulo, kuti Iye adzathe kubweretsa ana ambiri kwa Mulungu. Immanueli nafe. Anthu a Kuwala kwamadzulo, izo zikanadzawakopa iwo.

¹⁰³ Pamene Mulungu anapereka chizindikiro, “Ichi chidzakhala chizindikiro. Mulungu azidzakhala mu thupi.” Iye ankaganiza kuti izo zikanadzawakopa anthu. Izo zinatero. “Pakuti onse amene anamulandira Iye, kwa iwo Iye anawapatsa Mphamvu kuti akhale ana a Mulungu.”

¹⁰⁴ Ndipo izo zikuyenera kukopa anthu a Kuwala kwamadzulo pamene Kuwala komweko kukuwonetseredwa. Mulungu ndi Khristu ndi mmodzi. Petro anati, “Zidziwike kwa inu, kuti Mulungu wamupanga Yesu yemweyu, Amene

inu munamupachika, zonse ziwiri Ambuye ndi Khristu.” Chizindikiro, choneneredwa zoipa, koma Kuwala kwamadzulo kuli pano.

¹⁰⁵ Monga mtumiki wa Uthenga yemwe ali malemu, pamene uthenga wa chipentekoste unayamba kugwa, malemu Dr. Haywood, basi asanati...Iye, ine ndikuganiza, sanati... Mwinamwake pamene iye anali pa chi indeinde chake, tsiku lina pamene Mzimu unamukhudza iye. Iye anali wa ndakatulo, pambali pokhala mlaliki. Iye anatenga cholemba chake ndipo analemba iyo.

Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo,
Njira ya ulemelero inu mudzaipezadi;
Mu njira ya madzi muli Kuwala lero,
Kumizidwa mu Dzina lofunika la Yesu.
Ana ndi aakulu, lapani machimo anu onse,
Ndipo Mzimu Woyera ndithudi udzalowa;
Pakuti Kuwala kwamadzulo kwabwera,
Ndi zoonza kuti Mulungu ndi Khristu ndi
mmodzi.

¹⁰⁶ Kuwala kwamadzulo! Ngati ife tikuyenda mu Kuwala kwamadzulo, chizindikiro cha madzulo, ndiye kukuyenera kukhala Kuwala komweko ndi chizindikiro chomwecho, chizindikiro Chamuyaya. Ndiye zizindikiro zomwezo zidzatsira Kuwala kwamadzulo. Psyii! Kodi inu mukuchiwona Icho? Inu mukutha kuchimvetsa Icho? Umenewo ndi Uthenga Khristu ino. Kuwala kwamadzulo, zizindikiro za Mesiya zikutsatira Iwo, zikutsatira Uthengawo. Kuwala kwamadzulo kuli pano.

¹⁰⁷ Iko kukuyankhulidwa zoipa. Iwo adzakukanani inu, abale anu. Nndani anamukana Iye? Abale ake. Iwo anakonda kumamuwona Iye akupanga zodabwitsa. Koma pamene anadzafika pa Kalvare, kodi onse aja anali kuti? Pamene zifika panthawi yovutitsitsa imeneyo, pamene Mulungu mu Choonadi Chake ndi Baibulo Lake akuyenera kuwonetseredwa, iwo ali kuti? Iwo amabwerera mmbuyo.

¹⁰⁸ “Padzakhala chizindikiro chidzaperekedwe kwa inu. Ndipo zizindikiro izi zidzatsatira. Ntchito zimene Ine ndikuchita, inunso mudzazichita; ngakhale zochulukira kuposa izi, pakuti Ine ndikupita kwa Atate Anga.”

¹⁰⁹ “Padzakhala Kuwala kenanso mu nthawi yakumadzulo.” Oh, tsiku la mdima ili limene ife tadutsamo! Koma kwa zaka forte mitambo yakhala ikuyalula, kudutsa mu kukonzanso koyamba, kwa kubweretsa Uthenga wakuti Mulungu ndi Khristu ndi mmodzi, wakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi. Iye anasankha kuti azikhala mu thupi la munthu. Ndipo lero iwo akumupanga Iye chinachake chitakhala pa mpando wachifumu, iwo akumupanga Iye chinachake cha

mbiriyakale isanayambe, ena a iwo amafuna kumubwezera Iye mmbuyo kukakhala wambalume, ena amafuna kumupanga Iye mneneri. Koma, m'bale, Iye ndi Mulungu mwa inu, Mulungu kuwonetseredwa mu thupi. Motani?

¹¹⁰ Iwo anadziwa bwanji kuti Iye anali Mulungu mu thupi? Iye anati, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye Ine ndakuuzani inu zolakwika. Koma ngati Ine ndikuchita ntchito za Atate Anga, inu mukhulupirire izo.”

¹¹¹ Ndipo tsopano chinthu chomwecho. Uthenga ukutsitsimutsidwanso mmasiku otsiriza, Uthenga wa Yemwe Iye ali, chimene Iye ali. Immanueli akukhala mwa inu, ndi ntchito zomwezo zimene Iye ankachita, kudziwonetsera Iyemwini kudzera mwa inu, zinthu zomwezo zimene Iye ankazichita. Iko ndi Kuwala kwamadzulo. Iko kumaneneredwa zoipa. Iyo ndi njira yovuta.

¹¹² Izo zinatanthauza chinachake kwa mnyamata mwini chuma, komabe mtima wake wanjala, kuti abwere kwa Yesu, ndipo anati, “Rabbi, kodi ine ndichite chiyani kuti ndikhale ndi Moyo Wamuyaya?”

Anati, “Usunge Malamulo.”

Iye anati, “Ine ndachita zimenezo kuyambira ndiri mwana.”

Anati, “Iwe ukufuna kukhala wamngwiro ndiye?” Anati, “Unditsate Ine.”

¹¹³ Koma iye anachokapo wachisoni. Iwo unali mtengo wokwera kwambiri. Ngati iye akanamupatsa Iye ndalama ndi kumumangira tchalitchi chachikulu kwinakwake, kukaziika yekha kukhala membala, iye akanachita zimenezo mophweka. Kodi inu simukuwona momwe izo zapangidwira lero pakati pa olemera? Uko kunali ena.

¹¹⁴ Osati olemera okha, koma osauka; ambiri a iwo ochokera ku maenje amatope, ndi zina zotero, iwo anakana chifukwa cha kutchuka. Chifukwa, Iye anali wosatchuka. Iye anali Immanueli. Iwo anati, “Kumeneko ndi kunyoza. Ameneyo—ameneyo ndi mdierekezi. Kumeneko ndi kuweringa maganizo. Ameneyo ndi—ameneyo ndi Belezebule.” Aphunzitsi a tsiku limenelo, mipingo yawo yaikulu, anati, “Zamkutu.”

¹¹⁵ Koma Mulungu anati, “Icho ndi chizindikiro Chamuyaya, chizindikiro chapamwamba, chizindikiro cha chizindikiro chonse, choti Mulungu ali ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumapeto a dziko lapansi.” Ndi chimenecho chizindikiro chanu chapamwamba. Icho chikuposa zizindikiro zonse. Icho ndi chizindikiro choyamba. Machitidwe 19, anthu amenewo anachita kubwerera ndi kudzachizindikira chizindikiro chimenecho, iwo asanalandire konse Mzimu Woyera, Machitidwe 19:5. Komabe, wokhulupirira amene anali ndi Baibulo, ndipo anali ndi mlaliki wabwino amene ankatsimikizira kuti Yesu

anali Khristu, komabe iwo asanabwere kwa Iwo...Ndipo atawona chizindikirocho, iwo anabwera ndi kudzabatizidwanso, kudzaikidwa manja pa iwo ndi kulandira Mzimu Woyera. Izo ndi zoon.

¹¹⁶ Koma mu nthawi ya Kumadzulo, Kuwala kuli pano. Ndipo Iko kukutsutsidwa. Iko kukusereulidwa. Iko kukuyankhulidwa zoipa. Mneneri anati Iko kudzaneneredwa zoipa, “Chopunthwitsa.” Kuneneredwa zoipa, kusereulidwa, kutsutsidwa; Immanueli mwa ife, akuchita chifuniro Chake kudzera mwa ife.

¹¹⁷ Oh, lero, m'bale wanga mwendamnjira, mlongo wanga, ukhulupirire chizindikiro chimenecho. Uyang'ane mu khola la mtima wako, ndipo uwone ngati ungakwanitse kunena mwa iwemwini. Uwone chizindikiro chimene azibusa anachiwona. Mulungu mu thupi, akukhala pakati pa osauka, osowa, okanidwa. Uwone ngati ungamvetse Izo. Mulungu mu mtima mwako, Mulungu *umu*. Upenye ndipo uwone ngati Iye akudziwonetsera Iyemwini molondola, mu kukoma ndi kufatsa, monga Iye anachitira.

¹¹⁸ Zaka pang'ono zapitazo, panali mtsikana amene anapita ku koleji, ndipo, ndi azimzake ambiri kumeneko, iye anadzakhala wamatama pang'ono kwambiri, anachoka ku zomwe anaphunzitsidwa ku dziko lakwawo lakale, kumakhala ngati mayi mu dziko lakwawo. Ndipo tsiku lina iye anaganiza, patadutsa zaka zina ziwiri, kuti akawachezere amayi ake kenanso. Iye anawalemba iwo kalata ndipo anawauza iwo kuti adzafika pa sitima yakuti ndi yakuti, kuti adzakumane nawo pa sitieshoni. Koma, iye anabwera ndi wamatama pang'ono wina limodzi naye. Ndipo iye anali atasanduka wamatama, iyemwini. Ndipo iye anamubweretsa mzake wina ndi iye, zimenezo zinali ngati chimodzi cha zosokonezeka za masiku amakono, odziwa zonse, a mma-tini.

¹¹⁹ Ndipo pamene iye anadzafika pa sitieshoni, pamene iye anayamba kutsika sitima, iye anayang'ana. Ndipo pamenepo panaima amayi ake, akuyang'ana ndi zonse zimene zinali mwa iwo, kuti awone pamene mwana wake anali. Ndipo pamene mtsikana amene anali ndi iye, amayi...anawawona iwo nkhope yonse ili ndi zipsyera, ndi manja awo onse okupsya. Ndipo iwo ankawoneka moipa, okalamba, ndipo ankawoneka mowopsya. Ndipo mtsikana amene anali ndi Mary wamng'ono, anati kwa iye, “Ndikudabwa kuti chinthu chowoneka mwachisoni icho ndi ndani?”

¹²⁰ Ndipo mtsikanayo anachita manyazi ndi amayi ake. Iye anati, “Ine sindikudziwa. Ine sindikudziwa kuti iye ndi ndani.”

¹²¹ Ndipo amayi ake, pamene iwo anamuwona mwana wawo, anathamangira kwa iye ndipo anaponyera manja awo momukumbatira iye, anayamba kumupsyopyona iye.

¹²² Iye anawakankha, anati, “Ine sindikukudziwani inu. Inu mwamupeza munthu wolakwika,” chifukwa iye sankafuna kuyanjana ndi munthu woteroyo amene wina wakenso akanakhoza kumuseka ndi kumusereula naye.

¹²³ Panadzachitika kuti panali munthu, kondakitala wa sitima, ataima pafupi. Iye anadzamugwira mtsikanayo paphewa. Iye anati, “Manyazi pa iwe, iwe chinthu chomvetsa chisoni! Ine ndikuikumbukira nkhaniyo bwino bwino.”

¹²⁴ Ndipo anthu anasonkhana kuti amve chimene chinachitika. Ndipo iye anamugwira mtsikanayo, ndipo iye anati, “Mtsikana wamng’ono uyu, pamene iye asanafike usinkhu wa miyezi sikisi, anali mu kabedi kake kakang’ono mchipinda chapamwamba. Ndipo amayi ake ofunika, mkazi wokongola kwambiri amene ine ndinayamba ndamuwonapo,” anatero kondakitala wokalambayo. Anati, “Nyumba inayaka moto pamene amayi ake anali kuyanika zovala. Ndipo oyandikana nawo nyumba onse anathamangirako, akufuula. Iwo anawuwona iwo. Amayiwo sanazindikire konse izo. Iwo unali kumbali ya khonde la nyumbayo. Ndipo malawi anali atagwirira bwino, ndipo iwo anali atapita mmwamba.”

¹²⁵ Ndipo anati, “Iwo anakanika kumugwira mayi wotengeka uyo. Mwana wake anali mmwamba.” Ndipo anati, “Onse a iwo anafuula, ‘Inu simungadutse umo—mmalawi amenewo.’ Koma iye anatenga nsalu imene inali mdzanja lake, imene anali kuyanika, ndipo iyo inali nsalu yonyowa. Ndipo iye anafundira iyo, ndipo anapita kudutsa mu malawiwo, ndipo mmwamba, osaganizira za chiwopsyezo chake chomwe. Kenako pamene iye anakafika kumeneko, iye anadziwa kuti sangathe kudzifunditsa nsaluyo yekha pobwerera. Koma, kuti apulumutse kukongola kwa mwana wake amene anali woti amutengera iye, iye anamukulunga mwanayo mu nsaluyo, ndipo anathamanga kudutsa malawiwo, ndi nkhope yake yosafunditsa ndi manja ndi mikono. Ndipo iwo anawotcha nyama pa thupi lake, ndipo zinakhwinyatitsa matsaya ake mpaka kufika pamafupa ake, ndipo zinamunyasitsa iye, anawotcha tsitsi lake lonse, ndipo a— a . . . ponse mpaka ku mafupa a chala chake.”

¹²⁶ Anati, “Iye anadzakhala wosawoneka bwino, kuti iwe udzakhale wokongola. Iye anapereka kukongola kwake, iye anapereka chirichonse chimene iye anali nacho, kuti akupulumutse iwe. Ndiyeno iwe ukuima ndi kumachita manyazi ndi amayi ako ofunika?”

¹²⁷ M’bale, pamene ine ndimuwona Mulungu, Mulungu Wakumwamba, anasiya mpando Wake wachifumu, kukongola Kwake, ndi zonse zimene Iye anali; kuti adzabadwire pamwamba pa mulu wa ndowe, nkudzakulungidwa mu chovala cha pagoli, kuti adzasekedwe ndi zizindikiro Zake ndi zodabwitsa Zake, kuti adzatchedwe mdierekezi; kodi ine ndingamachite

naye manyazi Iye? Ayi, bwana. Lisiyeni dziko lamakono lichite chimene iwo akufuna kuchita. Kwa ine, Iye ndi chizindikiro chapamwamba. Mzimu Woyera mwa ine umafuula mokweza. Iwo ukhoza kundipangitsa ine kupanga mwachirendo ndi kukhala munthu wamisala, ndi dziko ili, koma ine sindingamukane Iye Amene anandipangira ine zochulukana. Iye anatenga malo anga mu imfa. Iye anatenga malo anga pa Kalvare. Iye anachita zinthu zonse izi. Iye anatsika kuchokera Kumwamba, kuchokera pa mpando wachifumu woyera wangale, kuti adzakhale munthu; kuti adzalawe kuvutika kwanga, kuti adzadutse mayesero anga, kuti adzadziwe momwe angakhalire mkhalapakati woyenera mwa ine, kuti azidzanditsogolera ine ndi kundilondolera ine ku Moyo Wamuyaya. Ndipo kudzera mu umphawi Wake, ine ndinapangidwa kukhala wolemara. Kudzera mu imfa Yake, ine ndapatsidwa Moyo, Moyo Wamuyaya.

¹²⁸ Musamukane Iye. Musachite naye manyazi Iye. Musachite naye manyazi Iye. Koma muzimufungatira Iye, ndikuti, “Inde, Ambuye wanga Wokondedwa, mupereke kwa ine monga iwo anachitira pa Tsiku la Pentekoste, Ambuye. Mupereke kwa ine Mzimu Woyera. Muwutsanulire Iwo mu mtima mwanga. Ine sindikusamala zimene a zaka zammadini akunena. Ine sindikusamala zimene dziko likunena. Ine sindikuyang’ana kwa iwo. Ine ndikuyang’ana kwa Inu.” Ndi chiyani chimenecho? Kujowina tchalitchi? Ayi. Chizindikiro chapamwamba, Immanueli, Mulungu nafe.

Tiyeni tipemphere.

¹²⁹ Mwa omvetsera mwa anthu mmawa uno, alipo ena muno amene angafune kunena kuti, “Kwa ine, ine ndikuchita manyazi ndi moyo wanga. Ine sindikuchita naye manyazi Iye. Ine ndikuchita manyazi ndi moyo wanga,” kuti ndiwupereke kwa Iye Amene anapangidwa wosawoneka bwino, ndi wonyozedwa ndi dziko?

¹³⁰ “Munthu wa chisoni, wodziwa zowawa. Ife tonse tinabisa nkhope zathu kwa Iye,” anatero mneneri. “Iye ananyozedwa ndi kukanidwa. Komabe, ife tinamuyesa Iye wokanthidwa ndi woenyedwa wa Mulungu. Komabe, Iye anavulazidwa chifukwa cha mphulupulu zathu, ndipo anamenyedwa chifukwa cha kusaeruzika kwathu; chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye, ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.”

¹³¹ Kodi inu mungachite manyazi ndi Iye? Ngati inu mukutero, bwerani paguwa ndipo mudzalape tchimo lanu. Ngati inu simukuchita manyazi ndi Iye, ndipo mukuchita manyazi ndi moyo wanu umene inu mwaupereka kwa Iye, chinthu choipa chotero. Inu mwachititsidwapo manyazi nthawi zambiri, pamaso pa abwana; pamaso pa mzanu wa mkazi, pamaso pa mzanu wamwamuna, pamaso pa bwenzi wanu wamkazi kapena bwenzi wamwamuna. Inu mwachitapo manyazi ndi Iye, Immanueli

akukhala mwa inu. Kwezani manja anu ndipo munene, “Mulungu, ndikhululukireni ine pochita manyazi.”

¹³² Ambuye wathu ndi Mulungu wathu, ife modzichepetsa ndi mwachisomo kwambiri tikukupemphani Inu kuti muvomeze kupepa kwathu, mmawa uno, chifukwa cha zolephera zathu zonse, pakuti tonse a ife nthawi zina timakhala olakwa. Ife ndi olakwa chifukwa choimira Choonadi. Ife ndi olakwa. Pamene iwo amafuna kutitchula ife dzina lina loipa, monga, oh, “woyera wodzigudubuza,” kapena chinthu china choipa chimene sichiri chomwecho, komabe nthawizina timabwerera mmbuyo monga Petro ndi kukadzitenthetisa tokha pa moto wa mdani. Mutikhululukire ife, Ambuye.

¹³³ Chaka chatsopano chikutiyandikira ife. Tiloleni ife tiyambire pa ora lomwe lino, ndipo tiwone chizindikiro chapamwamba cha Mulungu pakati pathu, Mulungu chikukhala nafe, chikukhala mwa ife, chikuchitachita, chikuchita ndendende mmene Iye ankachitira. Ndipo Kuwala kwamadzulo kuli pano.

Tikhululukireni ife zolephera zathu. Khululukirani machimo athu.

¹³⁴ Ndipo ife mwachisomo kwambiri, Ambuye, mulandire Mphatso Yanu ya Khrisimasi, Mwana wa Mulungu, kuti akhale mu thupi lathu, fumbi lathu, kuti azikhala ndi ife, kumayeretsa njira Yake mwa Magazi Ake Omwe, ndi kutipatsa ife chitsimikizo cha Moyo Wamuyaya. Ife tikukuthokozani Inu. Ine ndikukuthokozani Inu, Ambuye, chifukwa cha Mphatso yaikulu yopambana iyi yochokera kwa Mulungu, pakuti Iyo ndi mphatso, mphatso ya Mzimu Woyera, zonse zitaikidwa mu Dzina la Ambuye Yesu. Ndife okondwa kuilandira Iyo. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa mpingo wathu umaima ndi chizindikiro chimenecho, chifukwa chizindikirocho chimaimira Chiphunzitso cha Mpingo. Ife timaima ndi Iwo. Iwo umatiyimira ife. Ndipo izo ndi zodziwika pakati pa Akhristu kudutsa mdziko lero, za gulu la anthu osauka, osaphunzira pa 8th and Penn Street, ku Jeffersonville; kuti Immanueli, Lawi la Moto lochokera kuchipululu, Yesu waku Galileya, Mzimu Woyera wa pa Pentekoste, akuwonetseredwa ndi zizindikiro zonse za Emmanueli mu Kuwala kwamadzulo. Ndife othokoza kwambiri, Ambuye. Ndipo mulole kuti ena awone Iwo ndipo awulandire Iwo. Pakuti, ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, ndi chifukwa Chake ndi chifukwa cha Mpingo. Amen.

¹³⁵ Ine ndikanakonda ndikanakhala ndi mawu a woyimba. Ngati ine ndikanakhala ndi mawu a woyimba pano, ine ndikanakonda ndikanakuimbirani inu nyimbo imene ndimaikonda, yolembedwa ndi mzanga wofunika, William Booth-Clibborn.

Kutsika kuchokera ku ulemelero Wake, nkhani
ya moyo monse,
Mulungu wanga ndi Mpulumutsi anadza,
ndipo Yesu linali Dzina Lake.

Anabadwira mu khola, kwa Ake omwe
mlendo,
Mulungu wachisoni, misonzi ndi
mikwingwirima.

O momwe ndimkondera Iye! Momwe
ndimuyamikira Iye!

Moyo wanga, kuwala kwanga, zonse mu zonse
wanga!

Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi
wanga,

Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu
chikukhala mwa Iye.

Kudzichepetsa kotani, kutibweretsera ife
chiwombolo;

Pamene mu kufa kwa usiku, chiyembekezo
chimodzi chosawoneka; (Kenako mphenzi ya
mphanda inabwera!)

Mulungu, wofunika, wachikondi, anasiya
ulemerero Wake,

Kutsikira mu khola, modyetsera modzadza ndi manyowa,
kuti adzabadwiremo.

Kutsika kuti akope, apambane ndi
kupulumutsa moyo wanga.

O momwe ndimkondera Iye! Momwe
ndimuyamikira Iye!

Mpwewa wanga, kuwala kwanga, zonse mu
zonse wanga!

Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi
wanga,

Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu
chikukhala mwa Iye.

¹³⁶ Ndiyeno Iye ali mwa ine, ndipo ine ndiri mwa Iye. Ndipo
mwa inu . . . “Mu tsiku limenelo, inu mudzadziwa kuti ine ndiri
mwa Atate, Atate mwa Ine, ndipo Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine,”
Mulungu, Immanueli, nafe.

¹³⁷ Anali Immanueli ameneyo amene anamuwona George
Wright, atakhala pansu uko pompano; atagona kumeneko akufa,
pamene madokotala foro anamudutsa iye. Anali Immanueli
ameneyo, pamene Iye anachita kubwereka chiberekero, pamene
Iye anachita kubwereka ma—manda. Iye anabwereka maso
anga, anati, “Pita ukamuuze M’bale George, ‘PAKUTI ATERO
AMBUYE. Iye adzakumba manda a alaliki amenewo ndi zinthu
zimene zikumuseka iye.’”

¹³⁸ Anali Immanueli ameneyo. Anali Mmodzi yemwe uja, za nyama zazing'ono, tsiku lina mu thengo. Anali Mmodzi yemweyo, za Margie Morgan wakhala apo, ena onse. Anali Mmodzi yemwe uja amene anabwereka ubongo, zokhudzira za mthupi, kuti akadzipereke Yekha kwa dziko lero, kudzera mwa inu, pamene Kuwala kwamadzulo kukuwala. Mulungu atichitire chifundo, mzanga.

¹³⁹ Ine ndikutenga nthawi yanu yochulukuka. Tiyeni tiyese iyo. Tipatseni ife poyambira, "O momwe ndimkondera Iye!" Ndi angati akuidziwa iyo?

O momwe ndimkondera Iye! Momwe
ndimuyamikira Iye!
Moyo wanga, kuwala kwanga, zonse mu zonse
wanga!
Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi
wanga,
Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu
chikukhala mwa Iye.

[M'bale Branham akuyamba kung'ung'udza *Kutsika Kuchochera Ku Ulemelero Wake*—Mkonzi.]

Momwe ndimuyamikira Iye!
Mpweya wanga, kuwala kwanga, zonse mu
zonse wanga!
Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi
wanga,
Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu
chikukhala mwa Iye.

¹⁴⁰ [M'bale Branham akuyamba kung'ung'udza *Kutsika Kuchokera Ku Ulemelero Wake*—Mkonzi.] Tsopano ndi nthawi yoti Iye awonetsera chisomo Chake. Mayi akubweretsa khanda kuno, wa vuto lamagazi, khansa mu mtsempha wake wa magazi. Choipa icho kwa khanda?

Mulungu, pano pali liwu langa; yankhulani Mawu, ndipo zikhala chomwecho.

Pakuti, Ambuye, Inu munati, "Nenani kwa phiri ili, 'Suntha.' Musakaike. Izo zidzachitika."

Mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, ine ndikudzudzula mdierekezi uyu wotchedwa leukemia. Nthenda ya thupi la mwana uyu, iyo ichoka. Iyo ikuyenera kumusiya iye. Mu Dzina la Yesu Khristu, lolani zikhale chomwecho.

Dzuwa langa, zonse mu zonse wanga!
Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi
wanga,
Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu
chikukhala mwa Iye.

141 Momwe ine ndimkondera Iye! Ine sindingangozisiya Izo zizipita. Ine ndikufuna kutero, basi monga Yakobo, ndigwiritsitse kwa Izo.

... ndimuyamikira Iye!
Mpweya wanga, kuwala kwanga, zonse mu
zonse wanga!

“Ichi chidzakhala chizindikiro.”

Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi
wanga,
Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu
chikukhala mwa Iye.

142 Kodi Iye si wodabwitsa? Kodi inu simukumverera ngati muzingompembedza Iye? Basi mu Mzimu, kungompembedza Iye. [M’bale Branham akuyamba kung’ung’udza, *Kutsika Kuchokera Ku Ulemelero Wake*—Mkonzi.] Mungodziiwala nokha tsopano. Musachite manyazi. Mzimu Woyera uli pano. Umenewo ndi Mzimu Woyera. Basi mofatsa, mwa njira yanu yanu.

Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi
wanga,
Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu
chikukhala mwa Iye.

Ndi zimenezotu.

Kudzitsitsa bwanji, kutibweretsera
ife chiwombolo; (“Icho chidzakhala
chizindikiro.”)
Pamene mu kufa kwa usiku, chiyembekezo
chimodzi chozirala;
Mulungu, wofunika, wachikondi, anaika
pambali ulemelero Wake, (Taganizani za
chimene Iye anachita!)
Kuzitsitsa kuti akope, apambane ndi
kupulumutsa moyo wanga.

143 Tiyeni tikweze manja athu pamene ife tikuimba iyo.

O momwe ndimkondera Iye! Momwe
ndimuyamikira Iye!
Mpweya wanga, kuwala kwanga, zonse mu
zonse wanga!
Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi
wanga,
Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu
chikukhala mwa Iye.

144 Ambuye, ife sitidzatha konse kumvetsa chuma, chidzalo cha Mzimu Wanu, mpaka ife tidzamuwone Iye pa tsiku limenelo pamene Iye adzadza. Ife tikhoza kumadzagona mu fumbi. Ine ndikhoza kudzabwerera ku fumbi lapachiyambi, koma izo sizidzandidandaulitsa ine mpang’ono pomwe. “Ine ndikudziwa

kuti Iye adzaitana, ndipo ine ndidzayankha. Ndipo kenako ine ndidzamuwona Iye mmene Iye aliri. Thupi lachivundi ili lidzasinthidwa ndipo lidzapangidwa monga thupi Lake Lomwe la ulemelero, pamene Iye adzathe kulamulira zinthu zonse kwa Iyemwini.”

¹⁴⁵ Ine ndidzakhala woyamikira nthawizonse kwa Inu chifukwa cha mphatso ya Khrisimasi ya Khristu mu mtima mwanga, kudziwa kuti ndi Khristu yemweyo, chifukwa Iye akuchita chinthu chomwecho. Iye akundipangitsa ine kumverera ndi kumachita monga Iye anachitira pachiyambi, kwa wantchito Wake.

¹⁴⁶ Ndine wothokoza chifukwa cha Mpingo konsekonse, wogonjetsa, wokonzedweratu kale, ndi woitanidwa, ndi wosindikizidwa, ndi wodzodzedweratu ku Thupi limenelo. Ine ndimawapeza iwo mu Asia, Afrika, Rome, konsekonse, Indiana, kudutsa mu derali, Afrika. Konsekonse kuzungulira padziko, ine ndimawupeza Mpingo umenewo wogonjetsa, amene amadziwa kuti Inu mwabwera mu thupi. Ndipo Inu munanena kuti, “Mzimu uliwonse...” Mu Baibulo lanu, Inu munati, “Mzimu uliwonse umene suvomereza izi, ndi mzimu wolakwika, wotsutsakhristu. Mzimu uliwonse umene suchitira umboni chinthu chomwechi, kuti Khristu wabwera mu mnofu wathu, ndi mzimu wotsutsakhristu.”

¹⁴⁷ Atate Mulungu, ndithandizeni ine kuti—kuti ndiwa gwedeze ochirimika awo uko. Ine ndikukhoza kuwawona iwo, Ambuye, kutali uko. Ndikuwawona akhate pa zipata, ndikuyang’ana ku India kutali, pa Taj, pa chipata, zinthu zomvetsa chisoni izo zikukwawa pansu, opanda mapazi. Ndikuwawona anyamata akuda aang’ono osauka awo ku Afrika, manja awo aang’ono akufikira mmwamba. O Mulungu, nditumeni ine, Ambuye. Mulole Mngelo abwere ndi khala la Moto, ayatse mu solo yanga, Ambuye, ndipo muchotsepo litsiro lonse ndi ulesi, kuti ine ndikathe kupita ngati—ngati wochirimika wa Mulungu, kukawachotsa pa moto iwo amene ali mu mdima wokhudzika.

¹⁴⁸ Mudalitse mpingo wanga waung’ono, Ambuye. Oh, ine ndikutha kuwona kanjira kakang’ono ka utuchi kudutsa pana, ndi kuwona anthu ofunikirawo. Anthu akamadutsa mmagalimoto awo, kumawaseka iwo, chifukwa iwo akweza manja awo mmwamba, akumutamanda Mulungu. Koma tsiku lina Yesu adzabwera, ndipo zinthu zonse zidzakonzedwa. Ife sitimadzachita manyazi, Ambuye. Ife tidzalumikizana naye Paulo wakale, ndipo tidzati, “Ine sindikuchita manyazi ndi Uthenga wa Yesu Khristu, pakuti Iwo ndi Mphamvu ya Mulungu ku chipulumutso, ku Moyo Wamuyaya, kwa aliyense amene akukhulupirira.” Tithandizeni ife kuti tikhale moyo mwanjira imeneyo, Atate. Ife tikukupembedzani Inu tspano mu Mzimu,

mmalo Ammwambamwamba. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha kudzatichezera uku mmawa uno. Mu Dzina la Yesu. Amenii.

149 Kamodzinso, inu mutero?

O momwe ndimkondera Iye! Momwe ine . . .

Ambuye Yesu, . . .? . . . mu Dzina la Yesu.

. . . zonse mu zonse wanga!

Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi wanga,

Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu chikukhala mwa Iye.

150 Ndikungofuna zochuluka za Iye, sichoncho inu, Doe? [Delores akuti, “Inde.”—Mkonzi.] Ameneyo ndi mlongo wanga, mlongo wanga mthupi. “O momwe . . .” Mpongozi wanga wamkazi. Iwo akufuna zochuluka za Mulungu. M’bale Grimsley akubwera, akufuna zochuluka za Mulungu. “Zonse zanga . . .” Ndi zimenezotu. M’bale Wood, akubwera. M’bale Collins, mlaliki wa Methodist; mkazi wake, ena. “. . . anadzakhala Mpulumutsi wanga.” Izi ndi ntchito za Mzimu Woyera zikuitana, Iyemwini. “. . . akukhala mwa Iye.”

O momwe ine ndikunkondera . . .

Mungofotokoza izo mu njira yanu tsopano.

Momwe ine ndimuyamikira Iye!

Mpweya wanga, kuwala kwanga, zonse mu zonse wanga!

Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi wanga,

Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu chikukhala mwa Iye.

151 Ambuye, Ambuye, ndi awa apa, nkhosa za mu msipu Wanu. Adyetseni iwo, Ambuye, Mzimu Wanu. Iwo akudzipereka iwoeni kwa Inu, Ambuye. Iwo akudzipatulira miyoyo yawo kwa Inu. Iwo aimirira chifukwa iwo sakuchita manyazi ndi Uthenga wa Yesu Khristu. Ife tikudziwa kuti Inu muli pano, Lawi la Moto lalikulu, Khristu, Mzimu Woyera.

. . . -yamikira Iye!

Mpweya wanga, kuwala kwanga, zonse mu zonse wanga!

Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi wanga,

Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu chikukhala mwa Iye.

152 [M’bale Branham akuyamba kung’ung’udza *Kutsika Kuchokera Ku Ulemelero Wake*—Mkonzi.] Mungoyankhula mwa kuyankhula kwanu komwe tsopano. Umenewo ndi Mzimu Woyera umene wakubweretsani inu pano. Ingomuuzani Iye

kuti mukumukonda Iye. Mzimu Woyera womwewo umene unawakweza iwo pa Pentekoste, inu munaima apa mukulira, mukusisima, mukukondwerera.

Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi wanga,
Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu chikukhala mwa Iye.

Popanda kukaika, thupi ndi mwazi zinthu Zake, (khanda laling'ono mwa iye)

Iye anatenga mawonekedwe a munthu, anadzaulula dongosolo lobisika.

O chinsinsi chaulemelo, Nsembe ya Kalvare, Ndipo tsopano ndikudziwa Inu ndi "INE NDINE" wamkulu uja.

O momwe ine...O Mulungu! Momwe ndikumuyamikira Iye!

Mpweya wanga, kuwala kwanga, zonse mu zonse wanga!

Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi wanga,

Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu chikukhala mwa Iye.

¹⁵³ O chikondi chimene sichingandisiye ndizipita, chikondi chimene chimagwira mtima wanga kuposa chirichonse, kukoma kwa Kukhalapo kwa Mzimu Woyera; pamene mpingo Wake waima mozungulira guwa, ukupembedza, ukuyang'ana mu khola, ukuwona chinthu chomwecho chimene amuna anzeru anachiwona, Mulungu atasandulika thupi.

...anadzakhala Mpulumutsi wanga,
Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu chikukhala mwa Iye.

¹⁵⁴ Ngati pali chirichonse cholakwika mmoyo mwanu, muvomereze icho tsopano mu Kukhalapo kwa Mzimu Woyera, mwakachetechete. Muyang'ane mu mtima mwanu, muwone ngati muli khola mmenemo limene likhoza kupirira kunyozedwa, pa kuvomereza kwanu kuti Iye ndi Mulungu.

Chidzalo chonse cha Mulungu chikukhala mwa Iye.

¹⁵⁵ Ndi mitu yanu yoweramitsidwa tsopano, mungopereka pemphero, inueni. Uwu ndi Mzimu Woyera. Kodi inu simukumverera kufatsa ndi kudzichepetsa kwa Mzimu wa Mulungu, kukoma, Moyo wosatha?

¹⁵⁶ "Pamene pali malirime, iwo adzatha. Pamene pali ulosi, iwo udzalephera. Pamene pali chidziwitso, icho chidzalephera. Koma pamene chikondi chibwerapo, icho chimapirira kwanthawizonse." "Chikondi chimapirira motalika. Icho

sichimadzikweza chokha. Ichu sichimadzitukumula. Ichu sichimakhala khalidwe loyipa, losakhala bwino. Koma Ichu chimatichepetsa ife, chimatikometsa ife, chimaika kukoma mu solo yanu.”

¹⁵⁷ Tiyeni tipemphere tsopano, aliyense mu njira yanu yanu, kumuthokoza Mulungu chifukwa cha zimene Iye wachita.

¹⁵⁸ O Ambuye, mu kukoma kwa nyimbo iyi, kufotokozero mwa kaimbidwe, osati phokoso losamveka bwino, koma phokoso limene likutanthauza, kwa ife, Yemwe Mulungu wathu ali, monga Mawu afotokozero izo. Tsopano nyimbo ikufotokoza izo. Tsopano mitima yathu ikufotokoza izo, Ambuye, kachitidwe kathu pa Inu. Ife tikubwera patsogolo. Iwo ayima pa mapazi awo. Iwo amakukondani Inu. Pamodzi, Ambuye, ife tikuima ngati nkhosa Zanu, nkhosa za mu msipu Wanu. Ife timachikonda Chakudya ichi, Ichu ndi chabwino kwa miyoyo yathu. Ndipo ife tikudziwa kuti Mulungu amakhala ndi ife. Ife tikudziwa kuti Mulungu anakhuthuliridwa mwa Khristu, ndipo Khristu anakhuthuliridwa mu Mpingo.

¹⁵⁹ Ndipo pano ife tikuima lero, pamene mitundu yonse ya zipembedzo, ndi mitundu yonse ya—ya mabungwe ndi magawo, mitundu yonse ya tizikhulupiriro, komabe Mawu akudziyankhulira Okha, Mulungu akuwonetseredwa. Chizindikiro chapamwamba chakuti Mulungu akuwonetseredwabe mu thupi la anthu Ake, akupanga zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa, akuwonekera mu mawonekedwe a Mtambo, Lawi, kumakhala pakati pathu, kumazindikira mitima yathu, kumatiuziratu ife zinthu zimene ziri nkudza, kumachiritsa matenda athu, kumatipanga ife kukhala ofuna kupita Kumwamba kuti ife tidziwale ife. Mpaka, ife kufika popanga zinthu mwachirendo, kwa ana a mdziko; momwe iwo amaima ndi kumaseka, ndi kumaganiza kuti ife ndi amisala, chimodzimodzi basi monga iwo anachitira pa Pentekoste, kumati, “Kodi onsewa sanaledzere?”

Koma momwe ndimkondera Iye! Momwe ndimuyamikira Iye!

Mpweya wanga, kuwala kwanga, zonse mu zonse wanga!

Mlengi wamkulu anadzakhala Mpulumutsi wanga,

Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu chikukhala mwa Iye.

¹⁶⁰ Kodi inu mukukweza manja anu tsopano kuti mulonjeze chikhulupiriro chanu mwa Mulungu, malumbiriro anu kwa Mulungu, kukhulupirika kwanu ndi kukhala wowona kwa Mulungu, mpingo wonse?

¹⁶¹ Ife tsopano, Ambuye, tikudzipereka tokha kwa Inu, utatha mdalitso uwu wa kuwonetseredwa kwa Kukhalapo Kwanu,

kudziwa kuti Mulungu akuwonetseredwabe mu thupi lathu. Iye anadzakhala fumbi lathu, Iye anadzakhala thunthu lathu; Iye anadzidumphitsa Yekha kuchoka kwa Mulungu kuti adzakhale munthu, kuti munthu adzathe kukhala mwa Iye. Ndipo ife tinakumvererani Inu mmawa uno, mmizimu yathu. Ife tikuwona ntchito Zanu ndi kuwonetseredwa Kwanu. Ife timakukondani Inu. Ife tikudzipereka tokha mwatsopano kwa Inu: kuti tidzikulemekezani Inu, kuti tidzikukondani Inu, ndi kuti tidzichita chirichonse chimene ife tikudziwa mmene tingachichitire, chimene chingakhale chokusangalatsani, tidzikhala miyoyo imene ingakhale ngati Akhristu, imene singabweretse chitonzo, koma yokhala mdalitso ku Dzina Lanu Loyera lalikulu. Izi ife tikuchita, Ambuye, ngati ana Anu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

¹⁶² Ine ndikufuna kuti ndikufuneni inu chinachake inu musanakhale pansu. Kodi inu munayamba mwamvererapo chinthu chokoma chotero? Kukoma kwa Mzimu Woyera! Popanda aliyense kunena mawu; basi panokha kungodzuka, kubwera kutsogolo. Ulemelero wa Mulungu! Mukuona?

¹⁶³ Ine ndakhala ndikupemphera ndi kuwerenga, masiku awiri, pa izi. Kupitirira kuposa pamenepo. Kuyambira Lamlungu lapitalo, kapena lapita, eya, Lamlungu.

¹⁶⁴ Momwe kuti chizindikiro Chapamwamba icho, momwe Mulungu anati, “Ine ndidzawapatsa iwo chizindikiro. Ine ndidzakhala mu mnofu wawo. Ine ndidzakhala monga iwo; iwo adzakhala monga Ine.” Iye anati Angelo anasuzumira. Kapena anati... Angelo ananena kwa abusa, “Yang’anani mu kholamo, inu muwona chimene Ine ndikutanthauza.” Chizindikiro chimenecho sichinali cha Angelo okha. Ichu sichinangokhala cha abusa okha. Ichu ndi cha dziko, kuti liwone ndi kukhulupirira kuti Mulungu amakhala mu mnofu.

¹⁶⁵ Ndipo kudzera mu kupereka kwa thupi limenelo, Iye anayeretsa thupi lathu, kuti Iye akathe kukhala mkati mwathu. Mulungu mwa inu. Khristu mwa inu. “Taonani, Ine ndiri ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka kumapeto a dziko.” Musaiwale izi. Muzisunge izo mmitima mwanu.

¹⁶⁶ Ine ndalandira mpatso zina zopambana za Khristumasi, kamera ya kanema, ndi zinthu zina zambiri, mifuti ndi zinthu, zimene anthu amene amandikonda ine, iwo amandipatsa ine. Mmene ine ndikuyamikirira zimenezo!

¹⁶⁷ Koma, oh, uwu, Moyo Wamuyaya uwu, chitsimikizo chodala choti Khristu akukhala mwa ife, choti chidzalo Chake chikukhala mkati mwathu, zimatipangitsa ife kudzuka ndi kuchita mosiyana. Chifukwa, inu, pamene inu muchita zimenezo, inu mumadzakhala wothawathawa kwa zinthu za mdziko. Inu mumadzakhala mwendamnjira. Inu mumadzitenga nokha kuti ndi wakufa ku zinthu za mdziko, ndipo wamoyo mu

moyo watsopano. Tsopano inu ndi mlendo mu dzikoli. Ndinu mlendo chifukwa inu mwanena momveka, ndi machitidwe anu, kuti, “Ulipo Mzinda Wowumanga Wake ndi Wowupanga ndi Mulungu.” Mukuona? Ndipo inu simukusamalanso zinthu izi za mdziko, koma ife ndi anthu opita Kumwamba tikufunafuna Mzinda umenewo umene Wowumanga Wake ndi Wowupanga . . . wa Mulungu. Ife ndi Mbewu ya Abrahamu chifukwa ife takhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu, ndipo tafa ku zinthu za mdziko, ndipo taukitsidwanso mu chiukitsiro cha mawonekedwe Ake; kuti tiziyenda monga Abrahamu ankachitira, kufunafuna Mzinda uli nkudza, kuwatenga Mawu a Mulungu, kumachitcha china chirichonse chosiyana, kutchereza angelo pakhomo pathu, monga Abrahamu anachitira, amthenga a Mulungu, amene anabweretsa uthenga. Oh, ndi nthawi bwanji! Kumadzinenera kuti sitikufunanso kalikonse ka mdziko. Ife tikumufuna Iye, ndipo Iye yekha. Iye ndi Mpulumutsi wathu.

¹⁶⁸ Pamene inu muzipita kuchoka mchipinda chino mmawa uno, mutengeni Iye ndi inu. Musalole Iwo uchoke. Mukhale okoma mu solo yanu, masiku onse a moyo wanu. Mulungu akudalitseni inu tsopano pamene inu mukupita ku mipando yanu, ndipo ana ali ndi mphatso zawo. Mulungu akudalitseni inu.

¹⁶⁹ Kodi izi ndi zoti zipemphereredwe? Athandizireni iwo kufika kuno, mlongo. Tikhala tikupemphera.

Ambuye Mulungu mukhale wachifundo kwa m’bale uyu. Muchotse mzimu woledzera mwa iye, Ambuye. Mulole iye aledzere ndi Vinyo watsopano wa Mulungu. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

¹⁷⁰ Kodi izi si za Kumwamba? Ndi angati akumverera zimenezo, izi basi, kukoma chabe? Palibe amene akudziwa choti anene. Ine sindikudziwa kalikonse koti ndinene. Ndine basi—ndine . . . ine ndikusowa mawu. Ine—ine sindikudziwa choti ndinene. Basi Mzimu Wake ungoyenderera, mwaona.

¹⁷¹ Icho ndi chiyani? Inu mukusanduka ana ankhosa, ndipo Nkhunda ili pano kuti ikutsogolereni inu ku Chakudya cha ana ankhosa, Chakudya cha nkhosa. *Ichi* ndi Chakudya cha nkhosa, “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Mizimu yathu imakhala moyo pa Iwo.


¹⁷² Ine ndikuganiza tsopano ine ndiri woti ndiwonane ndi mzanga wabwino, Attorney Robinson, ngati inu mungadikirire pa chipindacho motalikirapo mpaka ine ndisinthe zovala zanga, ndikubwera, chifukwa ine ndiri ndi thukuta.

¹⁷³ M’bale Neville azipitiriza msonkhanowu tsopano, pa—pa mphatso za ana. Ambuye akudalitseni inu.

¹⁷⁴ Nthawizonse muziimba *Kutsika Kuchokera Ku Ulemelero Wake*. Pamene inu muzichita zimenezo, muzikumbukira chimene

ife timakhulupirira mwa Iye, “Chidzalo chonse cha Mulungu chikukhala mwa Iye.” Mulungu akudalitseni inu, M’bale Neville.

¹⁷⁵ [M’bale Neville akuyankhula ndi M’bale Branham—Mkonzi.] Eya, ngati inu mukufuna kuti ine nditero. [“Inde.”]

¹⁷⁶ M’bale Neville anandipempha ine ngati ndingabwereranso usikuuno, kenanso, kuti ndidzalalikire usikuuno kenanso. Ndimadana nazo zotenga msonkhano wake. Koma ine ndiri kuno, ndicho chimene ine ndadzera kuno. Chabwino, ine ndibwereranso usikuuno, Ambuye akalola, ndidzayankhule pa msonkhano. 

CHIZINDIKIRO CHAPAMWAMBA CHA59-1227M
(A Super Sign)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, wolalikiidwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, Disembala 27, 1959, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2020 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org